


NDICHOTIYENERA IFE

KUTI TIKWANIRITSE

CHIRUNGAMO CHONSE

 Nthawizonse chimakhala chamwayi kubwera ku nyumba ya Ambuye. Ine sindinayambepo, mmoyo wanga, ndawonapo nthawi imodzi imene ine ndinanong'onezapo bondo chifukwa chobwera ku nyumba Yake. Izo ndi a... Koma ine ndikuganiza kuti mmawa uno ndi pafupifupi nthawi yovuta kwambiri imene ine ndinayamba ndaifikapo. Inde, uko nkulondola. Chotero, zinthu zimachitika m'moyo, ife tikudziwa zimenezo, zimene timayenera kukumana nazo. Ndipo tikuyenera kukumbukira zimenezo, kuti izo zimafika kwa tonsefe.

² Ndipo ife tiri othokoza kwambiri mmawa uno, ine ndiri, ndipo ine ndikudziwa kuti abale anga ndi mlongo ndi oyamikira kwambiri kwa Mulungu, kudziwa kuti amayi athu ndi opulumutsidwa.

³ Ndipo iye ndi wokalamba, ndipo ife takhala tikuyembekezera izi kwa kanthawi, chifukwa iye ndi mayi wa ambiri, ndipo wawuphwasulira moyo wake pansu. M'masiku a amayi anga, iwo analibe zinthu zimene iwo ali nazo tsopano, zoti zivasamalire amayi pamene iwo anali ndi makanda awo. Mwinamwake, mwina, amayi amatha kubereka mmodzi wa ana mmawa umenewo, ndipo nkudzuka ndi kukachapa masana amenewo. Ndipo koma lero iwo amakhala m'chipatala masiku angapo, ndi mitundu yonse ya mankhwala, chimene chiri. Ife ndi othokoza chifukwa cha zinthu zoterozo zimene zingawathandize awa, amayi awa ndi onse.

⁴ Iwo ayandikira, kwambiri ndi imfa tsopano. Ndipo ine... [M'bale Branham akulira—Mkonzi]. Izo ndi basi—zopweteka pang'ono mmawa uno, komabe ine—ine ndinalonjeza kuti ndidzakhala kuno. Ndipo ndine...

⁵ Tsopano, sindinganene kuti amayi anga akupita. Nthawi zambiri ndanenapo izi. Ndipo ambiri ndi mboni, zokhudza masomphenya. Ine ndinati, “Ngati amayi anga omwe akanakhala atagona, akufa, ndipo nkuyang'ana pa nkhope yanga ndikuti, ‘Billy, chiyani—nchiyani chindichitikire ine?’” Ine ndinati, “Pokhapokha Mulungu atandiuza ine, ine sindingatziwe. Ine—ine sindingathe kunena.” Ndipo chinthu chomwecho chafika pochitika. Ngati amayi akupita, Iye mwamtheradi wandibisira ine.

Bambo anga asanamwalire, ndinawona masomphenya a iwo akupita.

⁶ Pamene ine ndinali ndikadali wochimwa, ine ndinamuwona mchimwene wanga, woyambayo, iye amapita.

⁷ Howard. Ine ndinakuuzani inu nonse, zaka ziwiri kapena zitatu iye asanapite, za kupita kwake.

⁸ Koma, amayi, Iye sananene liwu kwa ine. Ndipo ngati iye akupita, ndi chinachake chimene ine sindikuchidziwa. Ngakhale, ife tinali...Dokotala wanena kuti sanamvetsetse momwe iwo anakhalira moyo kudutsa Lamlungu lapitali. Ndipo iye ali mosauka kwenikweni. Koma, komabe, pamene ine ndinali...

⁹ Pafupifupi mwezi wapitawo, monga ine ndinachitira kwa Akazi a Broy; ine nthawizonse ndimakonda kuwafunsa anthu, podziwa kuti iwo ali pafupi ndi mathero, kuti ndingowona momwe iwo akuimira. Ife tikuyenera kukhala otsimikiza za izi. Ife sitikufuna kumangoti, “Chabwino, mwinamwake zonse ziribwino.” Ife tikufuna kukhala otsimikiza kuti izo ziribwino.

¹⁰ Ine ndinali ndi kuyankhulana kwabwino kwakutali m'mawa wina ndi amayi. Iwo anati, “Billy, ine—ine ndakhala moyo motalika mmene ndimayenera kukhalira.” Iwo anati, “Ine ndiribe china choti ndizikhalira moyo.” Iwo anati, “Ine ndiyenera kuti ndizipita.” Ndipo anati, “Ine kulibwino ndizingopita, ndikakhale ndi adadi ndi ena a ana enawo amene ali Kumeneko. Ine ndizikuwonani inu nonse, kawiri kawiri.”

¹¹ Ndipo pamene iye amaikidwa mu ambulasi, kuti azipita ku chipatala, kuti akawapatse gulukosi, chifukwa iwo samatha kudya kalikonse. Iwo amayenera kuwapatsa iwo gulukosi kudzera m'mitsempha yawo. Ndipo ine ndinati kwa iwo, pamene ife timawayika iwo mu ambulasi, ine ndinati, “Tsopano, amayi, chirichonse chiri bwino.”

Iwo anati, “Ine ndikulakalaka nditamapita.”

¹² Ndipo ndinati, “Amayi, ngati inu mukanandisiyira ine chuma pa dziko lapansi, cha madola handiredi millions, cha ife ana, kapena inu mukanatisiyira ife nyumba imene ikanachokera ku mzinda kukafika ku mzinda, izo sizikanakhala kanthu kuyerekeza ndi umboni uwu umene inu mukutisiyira ife, ‘Ine ndine wokonzeka kumapita.’” Ndi chuma chimene ndalama sizingagule, kudziwa zimenezo.

¹³ Chotero, pamaso pa zimenezo, ine ndikuyima molimba mtima, ndikukhulupirira zinthu izi zimene ndazilalikirira. Izi zikuyima bwino kwa amayi anga, zikuyima bwino kwa amayi a anthu ena, zikuyima bwino kwa tonsefe. Ine sindikanatha kunena kuti, “Mulungu, musawatenge iwo.” Chifukwa, ine ndikudziwa kuti mwamsanga pamene moyo wawo wachivundi

ukuchoka mu thupi ili, iwo ali ndi lina likuwadikirira. Ndipo iwo adzakhhalanso mkazi wamng'ono, mu maminiti pang'ono chabe iwo akangochoka kuno.

¹⁴ Kodi inu munayamba mwazindikirapo mwana wamng'ono pamene iye abadwa, akatumba ake aang'ono akugwedera ndi kunjenjemera? Koma pamene iye afika pa dziko lapansi, iye amalandira mzimu, ndipo kenako iye amadzakhala solo yamoyo. Ndipo mwamsanga pamene solo imeneyo ibwerera kuchoka ku thupi laling'ono ilo, pali lina limayembekezera ilo. Mukuona? Chifukwa, choyamba, Mulungu amapanga solo ndi mzimu, izo zimangopita ku matupi. Ndipo, ndipo pamene ife tichoka kuno, timangosintha malo okhalako ndi kupita ku ena. "Pakuti ngati msasa uwu wa padziko lapansi upasuka, tiri nawo wina kale ukudikirira." Koteru, ndicho chitonthozo chathu.

Tsopano tiyeni tipemphere.

¹⁵ Atate athu a Ulemelero, Akumwamba, kodi ife tikanachita chiyani mu maora awa a kusowa kwakukulu, ngati chikanapanda Inu? Koma chiyembekezero chathu sichinamangidwe pa china chirichonse kupatula Magazi a Yesu ndi chirungamo! Ndipo ndife okondwa kwambiri kudziwa kuti kuli Dziko kutsidya kwa mtsinje. Kuti pamene Inu mudzathana nafe pa dziko lapansi ili, kuti ife tidzangosintha malo athu okhalako, tidzapita ku Dziko laulemelero limenelo, kutsidya, kumene kulibeko matenda kapena kuwawa kwa mtima, imfa kapena kulekana. Ife nthawizonse tidzakhala tiri ndi Inu okonedwa athu. Chotero, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha chiyembekezo chaulemelero ichi chimene chiri pa chifuwa chathu lero.

¹⁶ Ndipo izo zimawoneka, Ambuye, zovuta mmawa uno kuti ine ndibwere kuno; osati kuti ndidzakutumikireni Inu, koma podziwa kuti ndine wamanjenje ndipo ndimadabwa momwe ine ndikanati ndidzafikire ku Uthenga uwu mmawa uno kwa mpingo, umene ine ndikumverera kuti Inu mwawuyika pa mtima wanga. Momwe mdani wanditengera ine mozungulira ndi mozungulira ndi iwo! Koma ine ndafika mpaka apa, ku guwa, mu Dzina Lanu. Ndipo ndikudzipereka ndekha, ndi Uthenga ndi zonse, kupita mmanja Mwanu, ndi podziwa kuti Inu ndi wokhoza koposa kuwutengera Iwo ku mtima uliwonse, ndi kupereka chirichonse chimene ife tikuchisowa. Ife tikuzipereka izo zonse kwa Inu tsopano, ndi ifeeni, monga utumiki Wanu; monga milomo yanga ili choyankhulira Chanu, ndi makutu monga zomvetserera Zanu. Tidalitseni ife, Ambuye.

¹⁷ Ndipo mulole kuti azimayi ena, azibambo, ndi iwo amene ati adzakhale mmasiku amene ali nkudza, ngati dziko liti lizidzaimabe, mulole iwo adzakonzekere ndi kudziwa, nawonso, kuti iwo akuyenera kudzafika kumeneko tsiku lina ku ora ili limene amayi afikapo. Ine ndikupemphera, Mulungu,

kuti iwo apange kukonzekera kwawo lero. Pakuti kulibeko chinthu chimodzi chinanso kudziko lapansi chimene chiri chofunikira. Kulibe ndalama zomwe zingagule, kulibe kutchuka komwe kungapitirire; kulibe chimene chingathandize koma Mulungu, ndipo Mulungu yekha. Ndipo ife tikugwira ku dzanja Lake losasintha, podziwa kuti Iye anati, “Mapazi a olungama amatsogoleredwa ndi Ambuye.” Kotero kuvutika kwapang’ono kumeneku kumene ife tiri nako tsopano, m’moyo uno, kudzatanthauza zazing’ono kwambiri. Monga wandakatulo anafotokozera izo, “Zovuta za m’njira sizidzawoneka ngati kanthu, pamene ife tidzafika kumapeto kwa njirayi.”

¹⁸ Tithandizeni ife, Ambuye, tilimbikire kukanikizira malo a maitanidwe apamwamba; podziwa kuti tsiku lina, mu kuseri kwakukulu kuno, ife tidzakakomana mokoma posachedwapa. Muwadalitse Mawu Anu tsopano. Muwadalitse antchito Anu. Mwana aliyense wa Mulungu amene ali muno, mulole mitima yawo ikhale yotentha ndi yokondowezeka mmawa uno. Ndipo, Atate, ine ndikufuna zina za izo, inemwini. Ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izo, zinthu zonsezi, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Amenii.

¹⁹ Tsopano ine ndinazindikira kuti apa ife tiri ndi mulu wa mipango. Ndipo ine ndiri. . . Ife tifika kwa iyo posachedwapa.

²⁰ Ine ndabwera kuchokera ku ulendo kumene ine ndakhala ndiri pa ulendo wokasaka, ndi mwamuna kumtunda uko kufupi ndi Alaska. Inu mukudziwa, nyengo ino ndi mtundu wa nyengo imene ndimaiyika padera, kugwa kwa masamba kwa mchaka, kuti ndidzimagenso ndekha, kukonzekera nyengo zimene ziri patsogolo za utumiki.

²¹ Ine si wamphamvu kwambiri, chabwino, ndinganene, m’mitsempha yanga. Ine ndiri ndi a—kachitidwe ka mitsempha koyipa kwambiri. Ndipo ine ndikuzindikira kuti zimatengera mtundu umenewo wa kachitidwe kuti kapange utumiki umene Ambuye andipatsa ine. Sungakhale ndi chirichonse mwaulemelero, padziko lapansi. Mwathupi, ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha thupi lamphamvu. Koma kachitidwe kanga ka mitsempha, chifukwa chakuti iwe umachita pamzere wapakati pa zathupi ndi zauzimu, ndi izo zimakukhadzula iwe mzdudutswa. Ndipo sindinayeserepo ndakhala pansii ndi kufotokoza zimenezo kwa osonkhana anga, chifukwa iwo sangazimvetse, chifukwa ine sindimadzimvetisa, inemwini. Koma ngakhale kwa madokotala, anandipima ine ndi kundipima kupsyinjika kwa mitsempha kumeneko; anati iwo sanawonepo chirichonse chonga chimenecho, mwaona, momwe zimasunthira kuchoka pamalo amodzi, mpaka njira yonse kupita kwa enawo. Ine sindimamvetisa kafukufuku wawo wasayansi ndi, kapena chimene iwo achita, njira zawo zochitira zinthu. Koma ine ndikudziwa kuti panali chinachake chimene

chinachitika kwa ine tsiku lina, pamene Khristu anandigwira ine, ine ndinasinthika.

²² Ndipo ndikungofuna kuti ndinene ichi, chikhoza kundilimbikitsa ine. Ichi chikuwoneka ngati icho chikhoza kukhala chinthu chosamvetsetseka kwambiri, kuchinena icho, mmawa uno. Koma basi, ndisanalowe mu Uthenga wanga, kuti ndikhale ngati ndadzitonholetsa ndekha, ine ndikufuna kunena zimenezo. Pamene ine ndinanena zakudzakhala kuno, ine sindimadziwa kuti amayi akanadzakhala akudwala.

²³ Ndipo inenso ndinapereka msonkhano wa usikuuno. Mulungu akalola, ife titero. Ine ndidzakhala pano usikuuno, ndikuyankhula, ngati izo ziri bwino ndi abusa. [M'bale Neville akuti, "Inde, bwana!"—Mkonzi]. Ndipo ine ndikufuna ndidzayankhule za, *Mtonthozi Wabwera*, usikuuno. Ndiyeno umenewo ndi msonkhano wa usikuuno. Ndipo ife tiri ndi msonkhano wa mgonero pano usikuuno. Ndipo anthu onse akuyitanidwa mwachikondi kuti abwere ndi—ndi kudzadya mgonero uwu ndi ife usikuuno, ndi ku Uthenga.

²⁴ Chinali chirimwe chapitachi pamene ndinali kumtunda ku Alaska, kapena kufupi ndi Alaska, ku British Columbia, ku . . . ku mautumiki, kuti Ambuye anatipatsa ife nthawi yaulemelero chotero. Ndipo ine—ine nthawizonse ndakhala ndikukonda kupita kunja.

²⁵ Kodi mukundimva bwinobwino kumbuyoko? Kodi . . . Ngati mungathe, kwezani mmwamba manja anu, kumbuyo uko.

²⁶ Nthawizonse ndakhala ndikukonda kupita kunja. Monga aliyense akulidziwira banja lathu, amadziwa zimenezo kumeneko. Amayi anga, amene akufa kunja uko tsopano, mayi awo anali Mmwenye. Ndipo kutembenuka kwanga sikunasinthe zimenezo, ndipo ine . . . kukonda kwanga kopita kunja; ndipo ndine wokondwa, chifukwa ndi kwinakwake kumene ine ndimamuwona Mulungu. Ine sindimapita kunja mochulukira kukasaka nyama, ndizo—ndi kukakhala kwandekha ndi Mulungu. Ndipo ine ndimasaka ndekha.

²⁷ Ndipo pamene ine ndinali kumtunda uko, ine ndinakomana ndi anamlondola amphamvu abwino. Amenewo ndi anyamata, mu Canada ndi malo, inu musanalowe mchipululu, bungwe la zinyama limakulumikizitsani kwa namlondola. Ndipo namlondola ameneyo amayenera kukhala ndi inu.

²⁸ Ndipo ine ndinakomana ndi m'bale wodabwitsa wa Chikhristu, wamng'ono, wachipentekoste, amene anali namlondola wotchuka mu Canada. Mkazi wake anali mkazi waulemelero, wopulumutsidwa. Ndipo iye ndi wausinkhu wa pafupifupi zaka forte zakubadwa, ndipo iye anali ndi ana faivi aang'ono, anyamata aang'ono, kuyambira eyitini kutsika mpaka pafupifupi usinkhu wa zaka ziwiri. Ndipo iye anali atapatsidwa

gawo lalikulu la mamailosi faivi-handirede a msewu waku Alcan, kukhala danga lake lolondolerako.

²⁹ Kuli Amwenye ena kumbuyo uko, amene sanafune kusamukako, ndipo iwo anali amwano kwambiri, ndipo anayika chikwangwani, “Mukabwera kuno, magazi adzakhetsedwa.” Koma, komabe, ife tinakwera kudutsa mopitirira icho, ndipo tinabwerera, chifukwa ine ndinkafuna kuti ndikayankhule ndi Amwenye amenewo. Kuwonjezera pamenepo, dzikolo linali lawo ilo lisanakhale lathu, inu mukudziwa. Ndipo ndinali ndi nthawi yabwino ndi iwo, Chirimwe chathachi, ndikuwauza iwo za Ambuye Yesu.

³⁰ Ndipo bambo wina wokalamba, bambo wokalamba wa fukolo, anali pafupifupi wa zaka handirede. Iye anali ndi ake. . . Ine ndimatha kuwona chifukwa chimene iye samafunira kuti apite. Iwo amakwirira akufa awo mu chipika, ndi kuchipachika chipikacho mmwamba mu mtengo. Iwo anali ndi ana aang’ono awiri atayikidwa mmenemo. Ndithudi, iye sankafuna kuchokapo. Ndikutha kuwona chifukwa chimene iye samafunira kuti achokepo. Ndipo osungawo, a—boma la Canada, Ulamuliro wa Canada unati, “Ngati iwo adzafika pomachita mwano, iwo adzangowachotsako kumeneko ndi kuwapangitsa iwo kumapita.” Bwanji, mumadana nazo kuti iwo azichita zimenezo; makanda awo atapachikidwa mmenemo mmitengo.

³¹ Ndipo kotero, komabe, mitsinje inatsikira mmusi ndi kudzatitchingira ife ndipo sitinathe kubwerreranso mdziko kumene ife tinkapita kuti tikasake chimbalongondo chotuwa. Bambo Southwick awa, Southwick iwo ali, anali namlondola. Ndipo iye. . . Ndipo ine ndinali ndi mtumiki wamng’ono, Eddie Byskal. Ndipo kotero mnyamata wake. . . Bambo Southwick anali ndi a—m’chimwene wawo wamng’ono wa, pafupifupi, pakati pa usinkhu wa zaka twente-faivi ndi sarte, anali atadwalika kwambiri ndi khunyu.

³² Bambo Southwick angokhala kumene Mkhristu, pafupifupi chaka chapitacho. Anali woweta ng’ombe m’mbuyomo, ndipo iwo amakhala ngati aukali, inu mukudziwa, mmoyo wawo. Ndipo, koma iye anali atangokhala Mkhristu kumene, ndipo iye ankakhulupirira. Ndipo iye anati, “Ine ndinawerenga bukhu lanu, M’bale Branham.” Ndipo ankapitiriza kukhomerera, motsatira, za m’bale wake wa khunyu. Iye anati, “Oh, ngati ine nditangokhoza kumubweretsa m’bale wanga kwa inu!” Chabwino, inu mukudziwa kumverera kumene izo zimakupangitsa iwe, iwe umakhala wopanda thandizo, sungachite kalikonse, ndipo umangodabwa momwe izo zonse zingachitikire.

³³ Ndiye mu Canada, kawirikawiri amuna amene. . . Inu amuna amene mumapita kunja mmaulendo, mumadziwa, pogwira akavalo. Ndipo ine ndimakonda akavalo ndi zinyama. Iwo

kawirikawiri amamangirira lamba kumchira, ndi kuwasiya iwo kumayenda mu mzere, mzere wothinana. Koma kumeneko inu simungachite zimenezo, chifukwa chimwalacho; kutaya kavalo mmodzi, ukhoza kutaya mzere wonsewo. Kotero ife timangoyenera kuwasiya iwo azipita, ndi kumalimbana nawo mnjira.

³⁴ Ndipo ine ndinali kutali kumbuyo uko, pa kavalo wamng'ono, ndikuyesetsa kulimbana ndi osocherawo ndi kuwabweretsa iwo mmenemo. Ndipo Mzimu Woyera, mu chisomo Chake, unatsikira pansi. Ine ndinamuyendetsa kavalo wanga, ndipo ndinakwera kudutsa chingwecho, kukwera mpaka kumene Bambo Southwick ankatsogolera, uko kutsogolo, kudutsa m'tchire. Ndipo ine ndinati, "Bud?"

Iye anati, "Inde, M'bale Branham."

Ine ndinati, "Kodi utenga mawu anga?"

Iye anati, "Ndi chirichonse chimene inu munganene."

³⁵ Ndipo ine ndinati, "Ine ndiri ndi PAKUTI ATERO AMBUYE kwa iwe." Ine ndinati, "Pita ukamutenge mchimwene wako kuchoka ku Fort Saint John," kumene kuli mamailosi seveni kapena eyiti handirede kutalikira kwake, "umubweretse iye pa msewu waukulu kuno." Ndipo iye ankakhala mkanyumba kakang'ono kokhala ndi sitovu yakale ngati mbaula, anali ndi ana ake mmenemo. Ndipo ine ndinati, "Nthawi yoyamba imene iye adzagwe khunyu, udzamuvule malaya ake ku nsana kwake. Ndikupatsa iwe chinachake choti udzachite. Udzawaponyere iwo pamoto, ndikunena kuti, 'Izi ine ndikuchita mu Dzina la Yesu Khristu.'"

Iye anati, "Ine ndidzachita zimenezo."

³⁶ Kotero iye anapita, anatumiza ndipo anakamutenga mchimwene wakeyo, anamubweretsa iye kumeneko. Ndipo mmawa umenewo iye ankayenera kuti achokepo azikatsatira mkukuluziwo, ndi bambo wina wosamalira zachirengedwe. Ndipo mchimwene wakeyo kawirikawiri amakhala ndi kugwa kumeneko kuwiri kapena kutatu, pa tsiku, ndipo amakhala nazo izo kuyambira ali mnyamata wamng'ono. Ndipo mkazi wake ankachita mantha pafupi kufa, ndi iyeyo, pamene iye akhala ndi kugwa khunyu kumeneko, chifukwa iye ankachita zosokoneza; wamphamvu kwambiri, mnyamatayo.

³⁷ Ndipo iye anagwa khunyu, Bud atachokapo. M'malo moti mkaziyo alumphire pa zenera, monga ankachitira nthawi zambiri, kuti awachotse ana ake pamenepo, iye anangolumphira pa iye, ndi kudzakoka malaya ake; mkazi wamng'ono, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, anakoka malaya ake ndipo anawaponyera iwo pa moto, ndipo anati, "Izi ine ndikuchita mu Dzina la Yesu Khristu." Iye sanakhalepo nazonso kuyambira pamenepo. Izo zinali mu chirimwe chathachi.

³⁸ Nthawi zambiri, ndikudziwa kuti zimakhala zovuta pang'ono. Anthu amene sangamvetse, amati, “M'bale Branham, nchifukwa chiyani inu mumapita kokasaka?” Mwaona, iwo samamvetsetsa basi. Palibe chifukwa chomayesera kuti ndizifotokoze izo, mwaona. Iwe umakapeza anthu kumeneko amene sangakhoze kupezedwa.

³⁹ Pafupifupi miyezi iwiri yapitayo, kapena osati motalika chomwecho, ndinadzutsidwa mmawa wina. Ine ndikukhulupirira, ine sindikutsimikiza, ine ndinazikamba izo kwa ambiri a mu mpingo. Alipo ambiri pano amene andimvapo ine ndikukamba izi zisanachitike. Ndipo mmasomphenyawo amene ine ndinawona, ine ndinawona chinyama chachikulu, chowoneka ngati mphalapala. Ndipo icho chinali ndi nyanga zazikulu, zazitali. Ndipo icho chinali... Ine ndinachita kuzungulira kumbali, ya thanthwe, monga *chonchi*, kuti ndifike kwa iyo. Ndipo iyo inali nyama yodziwika kwambiri. Iyo inali nyama ya chikho chopambana. Ndipo panali mwamuna amene ine ndinamuwona amene anali atavala malaya obiriwira, a mandalasi. Ndiyeno, tiri panjira, nditatha kuyigwira nyamayoyi, ine ndinamva a—liwu likunena kuti, “Nyanga zimenezo ndi zotalika mainchesi forte-thuu.” Izo ndi zotalika pafupifupi *chonchi*. Ndipo iyo inali nyama yaikulu kwambiri. Ndipo ndiri panjira ndikubwerera, ndinawona chimbalangondo chachikulu cha nsonga-za siliva zotuwa.

⁴⁰ Tsopano, chimenecho ndi chimbalangondo chodziwika. Ziripo zinayi m'banja la zotuwa. Chimodzi ndi cha nsonga za siliva, chimene chiri chodziwika. Chotsatira chimatchedwa, ndi dzina lachibadwa, *kadish* (?), chimene chimakhala chakuda, ndi khutu lozungulira; chachiwiri. Chachitatu, ndi chotuwa chawamba, chimene chimakhala pakati pa mtundu wakuda ndi bulauli, chimbalangondo chachikulu. Ndipo chotsatira ndi cha Kodiak, chomwe chimapezeka kokha pa Chilumba cha Kodiak chokha ndi—ndi kumadzulo kwa Alaska; icho ndi chachikulu, manthu, chachikulu mwa zimbalangondo zonse, koma icho ndi chotuwa. Koma cha nsonga ya siliva ndi chakuda, ndipo kuyera kumakhala pa... kutuwako kumakhala pamapeto pa nsonga ya tsitsi. Icho ndi chodziwika bwino, chamkwiyo kwambiri, chimbalangondo chakali.

⁴¹ Ndinachiwombera chimbalangondocho ndi kuwombera kwa mtima, ndinachipha icho. Koma ndinkaikayikira mfuti yaing'onoyo imene ndinali nayo, za kuyitenga iyo. Ndipo ine ndinali nditawauza abale. Ndi angati pano amene anandimvapo ine ndikunena za izo zisanachitike? Kwezani mmwamba manja anu. Chabwino, ndithudi, ambiri a iwo, mwaona.

⁴² Ndipo kotero ndiye Bambo Arganbright anandiyimbira ine ndipo ankafuna kuti ine ndipite ku Alaska. Chabwino, mmalo mopita ku Alaska, ine ndinamverera kutsogozedwa kuti

ndibwerere kuno ku ulendo uwu, kumtunda kuno ndi Bud, chifukwa ine ndinali nditamulonjeza iye.

⁴³ Pamene ine ndinakafika kumeneko, ine ndinamuwuza mkazi wake ndi anthu onse ozungulira kumeneko, zinthu izi zimene Iye ananena. Ine ndinati, “Koma, tsopano, ndani wa inu nonse amene ali ndi malaya obiriwira, amandalasi?” Palibe amene anali nawo. “Chabwino,” Ine ndinati, “ndiye ukuyenera kukhala ulendo wina umene ndidzayende. Koma, kwina wake, Ambuye adzapereka izo kwa ine, ndendende basi.” Kotero ine ndinati, “Ine ndimaganiza kuti mwinamwake ukanakhala ulendo uwu.”

⁴⁴ Chabwino, ife tinapitirira, pa ulendo. Ndipo tsiku loyamba, pamene ife tinakwera pamwamba, pamwamba pa mitengoyo, kumene kulibeko mitengo, kumtundako ku miyala, ndi akavalo athu. Ndipo tsiku lachiwiri, ife tinasaka zina, ndipo ife tinapeza nkhoa zambiri zokhala ndi nyanga zopiringizika makotala atatu, ndi zina zotero, koma izo sizinali zabwino basi.

⁴⁵ Ndipo inu kuyankhula za chiyanjano, aliyense wa ife wa chipentekoste ndipo tinali ndi Mzimu Woyera! Ife tinali ndi nthawi ina kumtunda kumeneko, ndi kumawona mitundu imeneyo ikusinthwa, ndi mapiri amenewo, ndipo kumtunda uko kumene Mulungu yekha amakhalako! Ndipo nthawi yabwino yotero! Sitimakagona mpaka itakwana wani koloko m'mawa, kumangomutamanda Mulungu ndi kumakhala ndi nthawi yaulemelero!

⁴⁶ Ndipo pa tsiku lachiwiri, ife tinatuluka. Ndipo pafupifupi mamailosi sikisi mmbuyo, uko kuseri kwa miyalayo, ife tinawona nkhoa zina zazikulu. Ndipo ndinati, “Chabwino, ife tibwerera mmbuyo, ndipo mmawa wotsatira masana ife tidzakhala pa njira yathu.”

⁴⁷ Chotero ife tinanyamuka mmawa wotsatira, kusanache; ndipo tinakafika, pofika naini koloko, ife tinali pamwamba kumene ife tinawona zibuluma za chipale.

⁴⁸ Koma tiri panjira yathu tikukwera, ine ndinali nditawona mphalapala yanga yamtchire yoyamba. Ndinali ndisanaiwonepo imodzi. Ine ndawonapo zoweta, ku Lapland, ndi zina zotero, koma osati mu mphalapala; zimene siziri . . . *Caribou* ndi dzina lachibadwa, ndi “gwape.” Ndipo kotero kawirikawiri zimakhala ndi nyanga zotambalala, monga *chonchi*, imodzi imapindikira kutsogolo kwa mphuno zawo, ndipo kenako nthambi zimatulukira kutsogolo; ndipo kenako nyangazo zimamangirirana, ndi nthambi zina zotambalala pafupifupi chomwecho.

Bud anali atandiwuza ine, “Mwinamwake . . .”

⁴⁹ Ine ndinati, “Ayi, ayi. Iye . . .” Ine ndinati, “Iyo siyinali mphalapala, chifukwa iyo inalibe nyanga za mtundu umenewo.” Koma mmawa umenewo, tikukwera mmwamba, bwanji, ine ndinawona ng'ombe ndi mwana wake. Ndipo ife tinapita ku

mbali imodzi, ndipo ine ndinaiwona iyo, ng'ombe yaing'ono yaimuna, ikuthamanga.

⁵⁰ Ndipo M'bale Eddie, akufuna kuti akawadyetse Amwenye kumene iye ali mmishonare. Apo panali mwamuna wabwino, akuchokera mnyumba yokondeka, ndi mkazi wongochokera kunyumba yokoma. Ndipo mikono yawo itadyedwa *apa*, ndipo ikupweteka, ndi utitiri, kumene iwo ankakhala ndi Amwenye ndi zinthu, kunja uko akuyesetsa kumubweretsa Khristu kwa Amwenyewo. Zimatengera chisomo kuti uchite zimenezo! Kumakadya chiponde kunja uko ndi manyuchi, ndi kumakagona mnyumba zimenezo momwe nsikidzi, utitiri ndi chirichonse, kumangodya izo monga choncho, komabe, kuti abweretse Uthenga wa Yesu Khristu!

Ndipo kotero M'bale Eddie anazembera kuzungulira phirilo.

⁵¹ Ndipo ine ndinakhala pamenepo mwamantha basi, kwa maora awiri, pamene ine ndinawona phiri lalikulu lodzaza ndi chipale pamwamba pake. Ine ndinaganiza, “Ambuye Mulungu, mudirole ine ndidzakhale kuno mu Zakachikwi.” Kuwona mbalame zachikasu zimenezo mmusi mwa phiri, ndi zitsamba zofiira, ndipo zonse zikumumikizana ndi mapiri aakulu okutidwa ndi chipale amenewo, akunyezimira mmusi kumalowa mnyanjazo. Pali chinachake basi cha izo, momwe inu mungakhoze kukhalira pamenepo ndi kumalira, ndi kumalira ndi kumalira, chifukwa ndi Mulungu yekha amene angakhoze kujambula zimenezo. Palibe chimene chingakhoze kuchita izo, mwaona.

⁵² Ndipo ine ndinali nditakhala pamenepo, ine ndinapezeka ndikuganiza, “Chabwino, ine ndikudabwa chachitika nchiyani ndi M'bale Eddie?”

⁵³ Ine ndinapita kwa Bud, ndipo iye anali atakhala pamenepo akusangalala nazo zimenezo, nayenso, pafupifupi maora awiri. Ndipo ife tinaimirira, ndipo ine ndinawona kamera ya kanema ya Eddie ili apo pomwe. Pamwamba pa mapiri amenewo, palibepo chirichonse koma mphalapala, ndele, ndele basi, ziri pamwamba pomwe mitengo siyingamere.

⁵⁴ Ndipo ine ndinamuzindikira iye mmusi mwa phirilo. Iye anali atakweza zala zake mmwamba monga *chonchi*, iye ankazembera mphalapala yaying'ono yayimuna iyi. Chabwino, iye—iye anayiwoembera mphalapalayo. Ndipo ife tinangoisenda iyo, ndipo tinabwereranso pamwamba pa phiri. Ndipo ine ndinatsika pansi mokwanira kuti tikapeze madzi.

⁵⁵ Ndipo ine ndinali ndikungoyang'ana pozungulira ndi magalasi. Mwanjirayina, pafupifupi mamailosi awiri kuchokera kwa ine, pamenepo panali nyama yangayo. Ine ndinamuwona iye. Ine ndinati, “Ndi imeneyo. Imeneyo ndi iyo.” Ine ndinati, “Tayang'anani apa, onani thanthwe ili, ife tikuyenera kuzungulira m'mbali.” Ndipo ine ndinati, “Chinthu chokhacho

chatsalira ndi a girini, amandalasi. . .” Ndipo ndinayang’ana, ndipo Eddie anali atavala malaya a girini, amandalasi.

Ine ndinati, “Eddie, ine ndimaganiza kuti iwe. . .”

⁵⁶ Iye anati, “M’bale Branham, ine sindimadziwa. Mkazi wanga ayenera kuti anawayika iwo mmenemo.” Iye anati, “Ndinavala malaya oyera mmawa uno, koma ine sindimadziwa zimenezo. Mkazi wanga akuyenera kuti anayika iwo mmenemo.” Mulungu samalephera chinthu chimodzi. Iye ndi mwangwiro basi. Pamenepo iye anali ndi malaya a girini, amandalasi.

⁵⁷ Namulondolayo anati, “M’bale Branham, ine sindikudziwa kuti muzungulira chotani kuti mukafike kumeneko.”

⁵⁸ Ine ndinati, “Sindikusamala ngati iye ali kutali mamailosi fifite, iye ndi wanga!” Ine ndinati, “Iye ndi wanga.” Ndipo ife tinayamba kuyenda mozungulira thanthwe limenelo, basi, oh, mtsetse *umenewo*, kumangozungulira m’mbalimo.

⁵⁹ Ndipo tinakafika kumeneko, ndipo ine ndinaipeza mphalapala yaikuluyo. Ndipo—ndipo m’malo moti iyo ikhale ndi nyanga zotambalala, inali ndi zobaya; sindinawonepo imodzi yonga iyo. Mukuona kusamvetsetseka kwake, momwe Mulungu amachitira zinthu?

⁶⁰ Kotero ife tinawauza anyamatawo kuti atsikire kumusi ndi kukatenga akavalowo ndi kukatenga nyamayo, ndi kudzakomana nafe kumusi pansi pamene tizitsika pansi. Chifukwa, M’bale Bud anayang’ana pozungulira, anati, “Masomphenya a M’bale Branham, ngati iwo anali owona okhudza m’bale wanga kuti achiritsidwa, ku khunyuu, iye ayipeza nyama imeneyo mosalabadira kumene iyo ili.” Chotero iye anati, “Inu mukangokumana nafe, ife tidzakhala tiri nayo iyo, tikamakatsikira kumeneko.”

⁶¹ Ndipo kotero pamene ife tinayisenda iyo; ndi chikopa ndi nyangazo, ndi zonse, zikanakwana pafupifupi mapaundi handiredede ndi twente-faivi; koma basi, osati chikopa cha thupi, chikopa chofewa basi. Kotero iye anati, “Tsopano, M’bale Branham,” anati, “Ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake.” Anati, “Sindimatha kuyisenda iyo apa,” iye ndi ine tonse awiri, mmodzi mbali iliyonse. Iye anati, “Inu mukuti nyanga izi ndi ‘mainchesi forte-thuu’?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Iye anati, “Izo zikuwoneka ngati nainte, kwa ine.”

Ine ndinati, “Izi ndi forte-thuu.”

Ndipo iye anati, “Ine ndiri ndi tepi yoyezera mchikwama changa cha chishalo.”

Ine ndinati, “Chabwino, inu muwona kuti izo ziri ndendende.”

⁶² Iye anati, “Ndiye, molingana ndi zomwe inu mwandiuzwa ine, penapake pakati pa kuno ndi kumene tikumane ndi anyamata amenewo, atavala malaya agirini amenewo, inu mupezako chimbalangondo cha nsonga ya siliva yotuwa?” Anati, “Sindinachiwonapo chimodzi, ndipo ine ndakhala m’mapiri amenewa moyo wanga wonse.”

Ine ndinati, “Koma izo ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.”

Anati, “Inu mukudziwa kumene icho chiri?”

⁶³ Ine ndinati, “Ayi. Koma icho chiri penapake pakati pa kuno ndi kuli anyamata amenewo.” Ife timatha kuwona kumusi komwe kumene iwo anali, pafupifupi mamailosi atatu, kumusi ku mzere wa mitengo. Ine ndinati, “Ife tikachipeza icho.” Tsopano, chimenecho ndi chinachake!

⁶⁴ Iye anati, “Ndiyeno, tikhala titafika kumusi uko mu ora ndi theka. Ndipo inu mukutanthauza kundiuza ine kuti mukapezako chimbalangondo chachikulu chotuwa chowopsya, cha nsongazasiliva, kwinakwake pakati pa kuno ndi kuli anyamata amenewo?”

Ine ndinati, “Izo ndi molingana ndi Mawu Ake.”

Iye anati, “Icho chiri pamenepo.”

⁶⁵ Chotero tinazikweza nyangazo, pamitu pathu, ndipo timakhwekhwereka ndi kumatsikira mmusi mwa phirilo, mpaka ife tinakafika ku zibuluma za chipale. Ndipo pamene ife tinafika ku zibuluma za chipalezo; kunali kotentha kwambiri, tinachita kulowa mu zibuluma za chipalezo pang’ono, kuti tizizidwe. Ife tinadutsa pamwamba pa chipalecho, tinadzatsika mpaka tinakafika pamene madzi ankatuluka pansu pa chipalecho, ndipo kumatsika mpaka ku . . . tinayamba kulowa mmitengo. Ife tinangokhala pansu, kuti tipume.

⁶⁶ Ine ndinatembenuka, ndipo ndinayang’ana. Ine ndinati, “Taona, Bud! Pafupifupi ngati ng’ombe, pafupifupi mamailosi awiri kutalikira kwake.”

⁶⁷ Iye anaponyera magalasi mmwamba, anayang’ana, anati, “M’bale Branham, kotero ndithandizeni ine, ndi cha nsonga ya siliva!” Anati, “Tayang’anani pa icho chikunyezimira mu dzuwa limenelo!”

⁶⁸ Ine ndinati, “Ndi chimenechotu.” Ine ndinati “Chabwino tiyeni tipite tikachigwire icho.” Kotero, izo ndi zomwe tinachita, tinapita ndi kukachigwira icho. Molingana, ndi masomphenyawo, nthawi inali itatha kwambiri kuti tichisende icho, ife tinkayenera kudikirira mpaka tsiku lotsatira.

⁶⁹ Ndiyeno titatha kuchipeza chotuwacho, tikubwerera mmusi, ndiye iye anati, “Ndipo inu munati nyanga zimenezo . . .” Anati, “Ngati nyanga zimenezo zikhale mainchesi forte-thuu, M’bale Branham, ine ndikomoka.”

70 Ine ndinati, “Iwe sukusowa kuti uchite kukomoka. Koma, izo ziri mainchesi forte-thuu, icho ndi chimene izo ziri.” Kotero tinatsikira kumusi kuti . . .

71 Ndipo ine ndinaganiza, mmasomphenya . . . Abale inu amene munakweza manja anu, ndi alongo, kanthawi kapitako, amene munandimva ine ndikunena izi izo zisanachitike. Ine ndinati akuyenera kuti anali Billy Paul. Anali mnyamata wamng’ono. Inu nonse mukukumbukira ine ndikunena zimenezo, ‘dzanja linalake laling’ono’? Koma mnyamata wake ali ndi zaka eyitini zakubadwa, ndipo monga usinkhu wa Billy Paul. Mukuona?

72 Ndipo pamene ine ndinakafika kumusi uko, apo panayima Eddie atavala malaya ake agirini, amandalasi. Ine ndinawona dzanja laling’ono limenelo likuzungulira nyanga zimenezo, ndipo pamene iye anapita kumeneko ndi kukatenga tepi yoyezera, anadzaiyika iyo pansu apa, ndipo anagwirizira, mnyamata wamng’ono ameneyo anadzayika manja ake. Ine ndinati, “Taona, Eddie, manja aang’ono amenewo pa nyangazo.” Ndipo pamene iye anadzakoka tepi yoyezerayo monga chonchi, iye anadzandiyang’ana ine ndipo anachita thovu kwenikweni pa kamwa, iye anati, “M’bale Branham, taonani apa! Kungokwanira basi, mainchesi forte-thuu, ndendende!”

73 Inu mukhoza kunena kuti, “M’bale Branham, chifukwa chiyani inu mukunena zimenezo pa Sande sukulu?”

74 Ine ndikunena izi pa chifukwa ichi. Kumbuyo uko mu Chipangano Chakale, anzeru akale ndi aneneri a iwo amene anapita, iwo anakapembedza Mulungu wa Kumwamba, Amene ankawawonetsera iwo masomphenya. Iwo ankamukonda Mulunguyo, kupyolera mu chisomo Chake, amene ankawakonda iwo. Iwo ankafunafuna Mzinda kwinakwake. Chinachake mkati mwawo! Iwo anasiya nyumba zawo ndipo iwo anadzakhala amwendamnjira, chifukwa iwo ankafunafuna Mzinda kwinakwake. Iwo ankanena zinthu zimene tikuziwona zikuchitika lero.

75 Mulungu yemweyo Amene ankawakonda iwo, ndipo mwa chisomo Chake, ndi kumawachitira iwo zinthu zimenezo, ndi Mulungu yemweyo amene ife tikumutumikira muno mu kachisi uyu mmawa uno, akuchita zinthu zomwezo. Ndipo pamenepo ilipo, mu chifuwa chathu, njala yofunafuna Mzinda umenewo, kwinakwake kumene iwo anapitako. Ndipo mwa Mawu Ake ndi mwa zizindikiro za Mphamvu Yake, ndi Mzimu womwewo ndi maulosi omwewo, chinthu chomwecho chimene Iye anawachitira iwo kumbuyo uko, Iye akutichitira ife lero. Ndipo inu mukuziwona izo ndi umboni wosalephera, kuti iye ndi Mulungu ndi Choonadi cha Mulungu.

76 Kotero, kulikonse kumene Mzinda wawukuluwo uli, ndipo kulikonse kumene iwo akusonkhanako, ine ndikuyembekezera kudzawawona amayi anga amene akufawo, ndi inu nonse ndi

iwo, uko mu Mzinda umenewo uko ndi iwowo: Abrahamu, Isaki, Yakobo, Daniele, Yesaya, Yeremiya. Chifukwa, chisomo chomwecho cha Mulungu chimene chinkawakonda iwo, ndipo kumawapatsa iwo masomphenya, ndi kumawawonetsera iwo zinthu zimene zinali nkudza, ndi Mulungu yemweyo lero amene akuchita chinthu chomwecho kwa ife, Choonadi chosalephera! Zimenezo, ndi Choonadi, mzanga.

⁷⁷ Atate wathu Akumwamba, ndife oyamikira. Chifukwa chimene Inu mumafunira kuti ndikhale ndi zinthu zimenezo, ine ndikuganiza, Ambuye, Inu mumangondilimbikitsa ine, podziwa kuti panali chodzidzimutsa chikubwera. Ine sindikudziwa; Inu mukudziwa. Ndipo ndikudziwa kuti sindineno mnyamata. Ine si mnyamata wamng'ono amene anakonda kukangamira pa epuloni ya amayi. Ndipo ndine mwamuna wazaka zapakati tsopano. Oh, momwe ine ndimakukonderani Inu, Ambuye! Momwe ine ndimakukhulupirirani Inu! Tipatseni ife chisomo tsopano. Tithandizeni ife kuti tiphunzitse Mawu Anu, kuti ena akhoze kuwona ndi kuphunzira, ndi kudziwa za Inu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

⁷⁸ Kwa mutu, m'mawa uno. Ine ndikuganiza kuti ndizo zonse zomwe ndinali nazo, basi. . . Chabwino, misonkhano usikuuno, mgonero, kutsukana-mapazi, ndi zina zotero, ndizo zonse. Ine ndakuitanani inu kuti mudzakhale ndi ife. Koma, kwa mutu wathu mmawa uno, tiyeni ife titsegule mu Baibulo, ku Mateyu Woyera, mutu wa 3, kuti tiwerenge gawo lina la Malemba. Ine ndikufuna kuti ndiyambire pa ndime ya 10 ya mutu wa 3 wa Mateyu Woyera.

⁷⁹ Ndipo ine ndikudziwa kuti alipo ambiri amene ayimirira, ndipo ife timadana nazo zimenezo; koma ngati ena a inu mungasinthane nawo iwo, kamodzi mu kanthawi. Ine. . . Mundikhululukire ine pokhala, potenga nthawi yanga, koma ine. . . Inu mukumvetsa. Tsopano kuwerenga kwa Lemba.

. . . tsopano ndiponso nkhwangwa yayikidwa pa muzu wa mtengo: chifukwa chake mtengo uliwonse wosabereka chipatso chabwino udzadulidwa, ndikuponyedwa pamoto.

Ine ndithudi ndikubatzani inu ndi madzi kuloza ku kulapa: koma iye amene akudza pambuyo panga ndi wamphamvu kundiposa ine, amene sindikuyenera kunyamula nsapato zake: iye adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera, ndi moto:

Amene chokupizira chake chiri mdzanja lake. . . iye adzayeretsa mwathumthu padwale pake, ndipo adzasonkhanitsa tirigu wake mu nkhowe; koma iye adzawotcha makoko ndi moto wosazimitsika.

Kenako anabwera Yesu waku Galileya ku Yordano. . . kuti adzabatizidwe ndi iye.

Koma Yohane anamuletsa iye, anati, ine ndikuyenera kubatizidwa ndi inu, ndipo inu mukudza kwa ine?

Ndipo Yesu poyankha anati kwa iye, Balola izo kuti zikhale chomwecho tsopano: pakuti kuyenera kwa ife kukwaniritsa chirungamo chonse. Ndipo iye anamulola iye.

⁸⁰ Ine ndikufuna kuti nditenge mutu kuchokera ku mawu amenewo pamenepo mu ndime ya 15.

. . . Balola izo kuti zikhale chomwecho tsopano: pakuti izo ndichoyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

⁸¹ Nthawi zambiri ndakhala ndikudabwa chifukwa chimene, Yesu waku Nazarete. . . Ndipo nthawi zambiri zakhala zikufunsidwa kwa ine. Nchifukwa chiyani Munthu ngati Yesu ankayenera kubatizidwa? Nchifukwa chiyani Munthu uyu anabatizidwa monga mwa mchitidwe wolapa ndi wovomereza, pamene Iye anali woyera, wopanda banga, Mwana wosayipitsidwa wa Mulungu wamoyo? Nchifukwa chiyani Munthu uyu ankayenera kuti abatizidwe ngati munthu wobwera? Ubatizo umachitika pambuyo pa kuvomereza. Iye analibe kuvomereza koti apange, chifukwa Iye anali Mulungu. Ndipo, Iye, nchifukwa chiyani Iye ankayenera kuti abatizidwe monga Iye anachitira, “ku kulapa,” chifukwa Iye sankasowa kulapa, pakuti Iye anali Mulungu wosalepherayo? “Iye anali m’dziko, ndipo dziko linapangidwa ndi Iye, ndipo dziko silinamudziwe Iye ayi.” Nchifukwa chiyani Iye ankayenera kubatizidwa?

⁸² Ndipo kodi munazindikira mawu a pambuyo pa zimenezo? Anati:

. . . pakuti chitiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

⁸³ Mwakuyankhula kwina, “Izo zikuyenera kukwaniritsidwa! Mawu onse amene Mulungu wayankhula, akuyenera kukwaniritsidwa!” Mulungu sanganene chirichonse popanda icho kukwaniritsidwa. Pamene Iye wayankhula Izo, iyo ndi ntchito yomalizidwa. Izo zimakhala zatsirizika kale pamene Mulungu wayankhula Izo. Mulungu samayankhula mpaka Iye atakonzekera kuti izo zichitike; ndipo, pamene Iye ayankhula, izo zimakhala ngati kuti izo zachitika kale.

⁸⁴ Tsopano, ngati izo sizingatipatse ife maziko oti tiyikepo chikhulupiriro chathu mmawa uno! Pamene Mulungu ayankhula Mawu, izo zimakhala zatsirizidwa kale. Nanga bwanji za malonjezo Ake amene Iye watipatsa ife? Chirichonse chimene Iye wanena, imeneyo ndi ntchito yomalizika kale. Chotero, ndiyeno, pamene ife tiwalandira Mawu Ake mu mtima mwathu, izo—izo zachitika kale, izo zatsirizika!

⁸⁵ Ndipo nchifukwa chiyani ndiye Iyeyo (izo sizikuyankha funsolo) anabatizidwa? Ambiri anenapo kuti, “Bwanji, Iye anabatizidwa chifukwa Iye anali chitsanzo chathu.” Zimenezo ndi zooni, mwanjira inayake, pa malo enaake. Zimenezo ndi zooni, koma izo zonse si Choonadi.

⁸⁶ Choonadi cha izo chinali, kuti Iye anali choyimira, Iye anali Wansembe Wamkulu. Ndipo wamsembe wamkuluyo asanadzozedwe, iye ankayenera kusambitsidwa.

⁸⁷ Ine ndikufuna ndikuwerengereni inu Lemba linalake, mphindi chabe, uko mu Bukhu la Eksodo. Ndipo ine ndikuganiza ndi ndime ya 29 imene ine ndinailemba; Mutu wa 29, kani. Ndipo ndikufuna kuti ndiyambire apa pa ndime ya 4 ya mutu wa 29.

Ndipo Aroni ndi ana ake aamuna iwe udzawabweretse pa khomo la kachisi la osonkhana, ndipo udzawasambitse iwo ndi madzi.

...iwe udzatenge—iwe udzatenge zovalazo, ndi kudzamuweka Aroni, ndi chikhotho, ndi mkanjo... ndi efodi, ndipo efodi, ndi chapachifuwa, ndi kuti mudzammange iye ndi lamba wa efodi:

Ndipo iwe udzayike nduwira pamutu pake, ndi pa opatulika...pa...korona pa nduwira.

Ndipo iwe udzatenge mafuta odzozera, ndi kudzawatsanulira iwo pamutu, ndi kumdzozza iye.

⁸⁸ Mwaona, Aroni, wansembe wamkulu, iye asanadzozedwe nkomwe, iye ankayenera kuti asambitsidwe ndi madzi. Chotero, pamene Yesu, Iye asanadzozedwe, Wamkulu Wansembe wathu, Iye anasambitsidwa ndi madzi.

⁸⁹ Ndipo kenako Mafuta odzozera amenewo anatsanuliridwa pa Iye, kuti amudzozze Iye. Monga Aroni anadzozedwa ndi mafuta; Iye anadzozedwa ndi Mzimu Woyera. “Pakuti Yohane anachitira umboni, powona Mzimu wa Mulungu ukutsika ngati nkhunda, ndipo nkudzapita pa Iye; ndipo Liwu linati, ‘Uyu ndiye Mwana Wanga wokonedwa mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhalamo.’” Chotero Baibulo linanena kuti, “Yesu anadzozedwa ndi Mzimu Woyera, ankapita akuchita zinthu zabwino.” Mwaona, Iye anadzozedwa.

⁹⁰ Ndipo Iye asanadzozedwe, Iye ankayenera kuti akwaniritse chirungamo chonse. Mwaona, Iye ankayenera kuti asambitsidwe ndi madzi Kudzozza kusanabwere pa Iye.

⁹¹ Ndipo icho ndi choimira chokongola kwambiri cha ife lero, monga ansembe kwa Mulungu. Ife timayenera kubatizidwa poyamba, kuvomereza machimo athu ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, kutsuka machimo athu; ndipo kenako inu mudzalandira Kudzozza, mphatso ya Mzimu Woyera. Mukuona, kusambitsidwa poyamba, ndipo kenako kudzozedwera ku utumiki. Palibe mtumiki wolowa paguwa asanabatizidwe

poyamba mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa, kulipo kokha...Kukhululukidwa kwa machimo kumakhalapo mu Dzina la Yesu Khristu basi, ayi, palibe dzina lina pansi pa Kumwamba linaperekedwa pakati pa anthu. “Kulapa ndi kukhululukidwa kwa tchimo ziyenera kuphunzitsidwa mu Dzina Lake, kuyambira ku Yerusalemu.” Uko ndi kumene Mzimu Woyera unagwera ndi kudzoza, koyambirira. Chotero, mtumiki kapena wokhulupirira aliyense amayenera poyamba asambitsidwe ku machimo ake, mu Dzina la Yesu Khristu; ndipo kenako nkudzozedwa ndi Mzimu Woyera, kuti abweretse umboni wa Mulungu.

⁹² Ndipo Khristu anali umboni wa Mulungu, chifukwa Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjaniitsa dziko kwa Iyemwini. Tsopano Iye anati:

...*Balola izi kuti zikhale chomwecho*, Yohane. Uko nkulondola.

⁹³ Mwa kuyankhula kwina, “Yohane, iwe ndiwe munthu wamphamvu, iwe ndiwe mneneri wamkulu, wamphamvu. Ndipo vumbulutso lako la Ine ndi Choonadi ndendende. Iwe ukudziwa Yemwe Ine ndiri. Iwe ukudziwa, chifukwa utumiki wako sunachokere kwa munthu. Utumiki wako unachokera kwa Mulungu. Iwe sunaziphunzire izo kwa munthu. Iwe sunaphunzitsidwe izi mu seminare. Koma pa, usinkhu wa zaka naini, iwe unapita ku chipululu, chifukwa iwe unabadwa uli mwana wosamvetsetseka, wachirendo. Ndipo kuyambira pa kubadwa kwako komwe, Mulungu anayamba kuchita nawe. Ndipo ngakhale usanabadwe, mneneri anakuwona iwe. Ndipo iwe ndi kuwala kwa tsiku lino. Ndipo mu chipululu...Iwe ukudziwa Yemwe Ine ndiri, chifukwa Mulungu, mu chipululu, anakuuza iwe kuti pakanadzakhala chizindikiro chikunditsatira Ine. Ndipo iwe wachitira kale umboni za Ichu, ndipo iwe ukuchidziwa ichu. Ndipo ife tikudziwa kuti wina ndi mzake ndi ndani. Ife tikudziwana wina ndi mzake. Ndiyeno izo nzoona kuti iwe ukuyenera kubatizidwa ndi Ine. Koma tiye tilole kuti izo zikhale chomwecho, pakuti, Yohane, ngati ife tiri kuwala kwa tsiku lino, ife tikuyenera kukwaniritsa chirungamo chonse. Mawu onse a Mulungu akuyenera kukwaniritsidwa ndi ife, a tsiku lino, pakuti chikuyenera kuti ife; chikutikakamiza, chikuyenera, ziri monga ife. Pakuti ngati ife tiri mboni zoonza za Mulungu lero, Yohane, ife ndi kuwala kwa m’badwo uno. Ndipo ngati ife tiri kuwala kwa m’badwo uno, pali Malemba ochuluka kwambiri amene akuyenera kukwaniritsidwa mu m’badwo uno. Ndipo ziri kwa ife!” Aleluya! “Ziri kwa ife, kuwonetsetsa kuti chirungamo chonse cha Mulungu chikukwaniritsidwa.”

Ndipo kodi chirungamo Chake ndi chiyani? Mawu Ake!

⁹⁴ Mwa kuyankhula kwina, “Yohane, iwe ukudziwa Yemwe Ine ndiri. Ine ndine Wamkulu Wansembe. Izo nzoona, Yohane,

ndipo Ine ndikuyenera kuti ndibatizidwe ndi iweyo. Koma ife tikuyenera kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Ndipo Ine ndikusowa kuti ndibatizidwe ndi iweyo tsopano, kuti ndikwaniritse Mawu a Mulungu, chifukwa Mawu onse akuyenera kuti akwaniritsidwe. Ndipo ife ndi kuwala kwa tsiku lino, ndipo ziri kwa ife kuti tikwaniritse zonsezi. Ndipo Ine ndikudziwa kuti chirungamo chako ndi chokhumba chako ndi kukwaniritsa Mawu. Izo zikuyenera kwa ife. Ife ndi kuwala.”

⁹⁵ Kuwala kwa m’badwo uliwonse kumayenera kuchita chinthu chomwecho. Ife tikudziwa chimene chikuyenera kukwaniritsidwa. Inu amene muli auzimu ndipo mukudziwa Mawu a Mulungu, mukuwona chimene Mulungu walonjeza. Tsopano Mawu sadzabwera mophweka chabe, koma Iwo amabwera mwa kuyang’anitsitsa, inu mumayenera kukanikizira njira yanu mkati kuti muwachite Iwo. Koma, komabe, zikutikakamiza ife, nkoyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse cha Mulungu. Ife tikuyenera kuchita zimenezo.

⁹⁶ Ndipo tsopano Yesu anazindikira, mwa Yohane, kuti Yohane anali mneneri wona. Mawu anali atayankhula za Yohane, ndipo Iye ankadziwa kuti iye anali mwamtheradi mneneri wa oralo. Ndipo Yohane ankadziwa kuti Yesu anali Mesiya, wa oralo. Ndiyeno iwo awiri onse anali ndi kumvetsetsa.

⁹⁷ Oh, ngati Mpingo wa Mulungu wamoyo ukanangotengera izo mmitu mwawo mmawa uno, ndi mmitima yawo; kuti Mpingo sudzalekanitsidwa ndi zotchinga za chipembedzo, kutsemphana kumeneko mu tizikhulupiriro ndi mitundu, ndi zina zotero; kuti ife tidzakhoze kubwera pamodzi mu Dzina la Ambuye Yesu, osakhala ndi chirichonse chotichotsa ife ku Mawu owona a Mulungu wamoyo; ndi kumayenda molunjika tikutsika mu mzere wa Lemba umenewo, kuti tikakwaniritse chirungamo chonse cha Mulungu cha lero!

⁹⁸ Pakuti, aliyense akudziwa kuti ife tikukhala mu Kuwala kwa kumadzulo. Mneneri anati, “Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo.” Ndipo kotero ife tikudziwa kuti ife tikukhala mu ora limenelo, ora la Kuwala kwa kumadzulo. Chotero, Ambuye Mulungu, tithandizeni ife kuti tizindikire zimenezo.

⁹⁹ Tiyeni tibwerere mmbuyo pang’ono chabe, ndipo titenge anthu ena amene anadziwa malo awo mu tsiku lawo, ndipo anali ololera kupirira kutsutsidwa kapena china chirichonse, kuti Mawu a Mulungu akhoze kukwaniritsidwa.

¹⁰⁰ Tiyeni timutenge, mwa chitsanzo, Nowa ndi tsiku lake. Kunali koyenera kwa Nowa, iye atatha kukomana ndi Mulungu ndikudziwa dongosolo la Mulungu la tsikulo.

¹⁰¹ Tsopano, iwe sungachite chirichonse pokhapokha utadziwa chimene iwe ukuchita. Iwe ukuyenera kudziwa kuti icho ndi chifuniro cha Mulungu. Iwe ukuyenera kudziwa kuti

ndi dongosolo Lake ndi chokhumba Chake, ndipo icho chaulidwa kwa iwe, zikatero palibe chirichonse chimene chiti chidzalepheretse zimenezo.

¹⁰² Tsopano, Nowa anadziwa, chifukwa iye sanapeze utumiki wake kuchokera ku sukulu ina ya maphunziro, koma iye anayankhulana ndi Mulungu maso ndi maso. Ndipo iye ankadziwa kuti kunkabwera chigumula cha madzi. Iye ankadziwa kuti mvula ikanadzavumba kuchokera mu mlengalenga, ngati mitsinje ikutseguka, ngakhale izo zinali molimba zikutsutsana ndi nkhani za sayansi mu tsiku limenelo. Asayansi, mosakaika, ankamutsutsa Nowa, ndipo anati, “Ife tikhoza kukutsimikizira iwe mwasayansi kuti mulibemo madzi mmwamba mmenemo.”

¹⁰³ Pakuti, iwo unali m’badwo wopambana nthawi imeneyo, wopambana kwambiri kuposa momwe ife tiriri lero, wasayansi kwambiri kuposa momwe ife tiriri lero. Inu mukudziwa, Yesu ankalozera kwa iwo, “Monga izo zinali m’masiku a Nowa.” Momwe iwo anamangira zosema ndi mapiramidi, ndi zinthu zimene ife sitingakhoze kuzikhudza, kuzimanga lero. Ndipo iwo anali asayansi opambana. Iwo anali ndi mitundu ndi zinthu, ndi mankhwala owumitsira mitembo, mu tsiku limenelo, kuti iwo ankakhoza kupanga thupi lisawonongeke. Ife sitingakhoze kuchita zimenezo lero ngati tikanati titero. Iwo anali atapita patsogolo kwambiri kuposa momwe ife tiriri. Ndipo iwo ankakhoza kutsimikizira kuti munalibe madzi mmenemo.

¹⁰⁴ Koma, chimodzimodzi basi, izo zinali zoyenera kwa Nowa, iye atatha kulidziwa dongosolo la Mulungu, kuti iye ankakhomabe zamphamvu chombocho, chimodzimodzi basi, pakuti iye ankadziwa kuti chombo chokhacho chikanakhala chinthu chokhacho chimene chikanati chidzayandame. Ziribe kanthu, ngati izo zinatsimikiziridwa mwasayansi kuti munalibe madzi mmenemo; ngati Mawu a Mulungu anali atanena kuti ikanadzavumba, iyo ikanati idzavumbe.

¹⁰⁵ Ndipo mudirole ine ndiyime apa kuti ndinene ichi, chifukwa cha anthu odwala. Ngati vuto lanu liri loyipa kwambiri kuti mwinamwake dokotala akunena kuti palibe chiyembekezo; kodi zimenezo zikupanga kusiyana kotani, bola ngati Mulungu akunena kwa iwe, “Ine ndikulola iwe kuti ukhale ndi moyo”?

¹⁰⁶ Nchifukwa chiyani...Dokotala kapena wasayansi wina akhoza kunena kuti, “Chipembedzo chako chimene iwe umachikamba, Mzimu Woyera, ndi kuyankhula mmalirime kwako, ndi kwako—ndi ziwonetsero zako, ndi zilubwelubwe chabe zammutu.” Kuti, “Iwe sunadzazidwe ndi Mzimu Woyera.” Kuti, “Kulibeko chinthu choterocho.” Ndipo masauzande ochuluka a azilaliki amalengeza izo lero, kuti, “Inu nonse mukungozichititsa.” Kuti, “Kulibeko chinthu choterocho.”

107 Ndipo izo ziri, ena a iwo anenapo kwa ine, “Bwanji iwe osajowina chipembedzo china chabwino, ndi kugwiritsa ntchito chikoka chako popititsira mtsogolo chipembedzo chimenecho?”

108 Ndipo kenako nkudzati, “Tsopano, gulu ili apa la chipentekoste limene iwe ukupusitsana nalo, iwo angokhala gulu la achipembedzo achinyengo chabe. Ndipo iwo—iwo... Kulibeko chinthu choterocho monga icho. Iwo angokhala otengeka mmalingaliro. Iwo—iwo—iwo alibe chimene iwo akuchikambacho. Ife tikhoza kutsimikizira kuti iwo alibe zimenezo.”

109 Oh, m’bale, inu mwachedwa kwambiri. Ife tikudziwa chimene ife tiri nacho! Ndife obadwa mwatsopano, mwa Mzimu Woyera, ndipo ife tikumawona ntchito Zake pakati pathu pomwe, chimodzimodzi monga momwe zinkakhalira mu nthawi ya Baibulo. Ngati inu mumakhulupirira mwa Mzimu Woyera womwewo, ndiye nanga bwanji Iye sakuchita chinthu chomwecho mu mpingo wanu? Chifukwa, Iye sangasinthe; Iye ndi Mulungu.

110 Kotero, ziribe kanthu kuti maumboni a sayansi ali motani, kuti ife tiri “otengeka chabe,” kuti ife “tangobalalika mmalingaliro,” kuti ndithudi “kulibeko kalikonse ku chipembedzo chachikulu ichi” cha ife, kuti “icho—icho sichiri basi chimene icho chiyenera kukhala,” ndi zina zotero monga chomwecho, kuti ife ndi “gulu chabe la otayidwa kunja,” musakhulupirire zimenezo! Musakhulupirire zimenezo!

111 Ngati mwana wanu wamkazi atabwera kunyumba kuchokera ku sukulu, ndi kudzati, “Amayi, ife tatsimikizira, lero, kuti—kuti chigaza cha munthu ndi chofanana basi ndi cha chimpanzee, mwaona.” Kapena, “Ife—ifetaphunzira ndipo—ndipo tadziwa kuti ife tonse tinachokera ku khungu limodzi, kuti ndife zinyama chabe.” Musakhulupirire zimenezo!

112 Ndipo ziribe kanthu chimene aliyense anena, wazafioloje aliyense, dokotala aliyense, wasayansi aliyense, mphunzitsi aliyense; inu mugwiritsitse ku Mawu a Mulungu! Pakuti, kumbukirani, ife tikumanga, monga, Nowa anali mu tsiku lake, ife tikumanga Chombo.

113 Ndipo Nowa ankadziwa kuti ngati samalizitsa chombo chimenecho, kuti si banja lake lokha limene likanati lidzapulumutsidwe. Kotero, iye ankadziwa dongosolo la Mulungu. Mkatikati mwa kutsutsidwako, izo sizinkamutsautsa iye mpang’ono pomwe. Iye ankapitiriza kumakhoma chombocho.

114 Kotero, ziribe kanthu ndi zochuluka bwanji zimene iwo akunena, “Kulibeko chinthu choterocho ngati ubatizo wa Mzimu Woyera. Kulibeko chinthu choterocho ngati machiritso Auzimu.” Chikutikakamiza ife, ndichoyenera kwa ife, kuti tikwaniritse

chirungamo chonse, kuti tiyime mu ora lino la yesero, ndi kukhomerera pa Chombo cha Ambuye!

¹¹⁵ Iwo amanena kuti, “M’bale, inu nonse mwasokonezeka mu maubatizo anuwo, ndi zina zotero. Pali... Inu simukuyenera kumabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu.”

¹¹⁶ Ine ndimayankhula ndi banja lokondeka madzulo apitawa. Ndipo pali mnyamata amene wangobatizidwa kumene, ndipo amakhulupirira kuti alipo Mulungu mmodzi yekha. Ndipo mu msonkhano wa Amuna Azamalonda iwo samamulola iye kuchitira umboni, chifukwa iye samakhulupirira kuti kuli Amulungu atatu.

¹¹⁷ Tsopano, ziribe kanthu zomwe iwo amanena, ndizokakamiza kwa ife, ndizoyenera kwa ife, kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Mawu adzakhalabe chimodzimidzi pamene mabungwe a Amuna Azamalonda ndi onse zidzapita, ndipo mipingo siidzakhalaponso. Mawu a Mulungu adzakhalapobe chimodzimidzi! Ndichoyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

¹¹⁸ Kodi aneneri sananenere za tsiku lino? Kumbukirani, otsutsa amenewo, ndikoyenera kwa iwo kuti akwaniritse zimenezo, nawonso, chifukwa izo zikuyenera kukwaniritsidwa, nazonso.

¹¹⁹ Koma, Nowa, izo sizinamusautse iye, iye anapitirira patsogolo chifukwa iye ankadziwa dongosolo la Mulungu. Iye ankadziwa chimene Mulungu akanati adzachte, M’bale Kidd. Iye ankadziwa dongosolo la Mulungu chifukwa iye anali atayankhulana ndi Mulungu, ndipo izo zinali molingana ndi Mawu a Mulungu, ndipo iye anapitirira kumachita zimenezo, mulimonse. Kaya sayansi imakhoza kutsimikizira izo kapena china chirichonse, kapena ndi kutsutsa kochuluka bwanji kumene kunayikidwa pa Nowa, iye anakhalabe molondola ndi Mawu a Mulungu, ndipo ankasemabe pamenepo. Chifukwa chiyani? Izo zinali zoyenera kwa iye, chifukwa Nowa anali mneneri. Ndipo izo zinali zoyenera kwa iye mwakuti iye anasunga, Mawu a Mulungu. Iye anakhala nawo iwo.

¹²⁰ Izo ndizoyenera kwa mneneri aliyense, mneneri wona wa Mulungu, kuti iye azikhala ndi Mawu. Mosalabadira zomwe sayansi inganene, ndi zomwe *ichi* chingatsimikizire *ichi*, kapena zina zotero, izo—izo—izo ndizoyenera kuti izo zikwaniritse chirungamo chonse.

¹²¹ [M’bale Branham mwakachetechete akuwerenga cholembedwa—Mkonzi]. Chabwino. Iwo atumiza mawu kwa ine kuti ndiwapemphere amayi pompano. “Muwapempherere iwo pompano. Dokotala wangochoka kumene.” Chabwino.

¹²² Tsopano, Ambuye Yesu, ine ndaima pano. Amenewo ndi amayi anga. Ngati iwo akupita, ine ndikuwupereka moyo wawo mmanja mwa Mulungu. Koma apa pali Uthenga umene ukuyenera uzipitirira, Ambuye. Pali amoyo pano amene

akuyenera—akuyenera kuti adzafe. Inu mundithandize ine, Ambuye. Ndine wanu. Mu Dzina la Yesu.

¹²³ Ndichoyenera kwa ife! Ndichoyenera kwa ine tsopano kuti ndikwaniritse chirungamo chonse. Mawu a Mulungu amabwera poyambirira! Palibe chikondi chonga chikondi cha Mulungu!

¹²⁴ Tsopano, Nowa, zinalibe kanthu kuti kutsutsako kunali kotani pa abambo Nowa, iye ankadziwa pamene iye anali atayima, ndipo kotero iye anakhalabe molondola ndi Mawu. Ndipo iye anamanga chombo kuti apulumutsiremo apanyumba ake, chifukwa chinali choyenera kwa iye kuti achite chomwecho. Icho chinali choyenera kwa Nowa, kuti—kuti achite chomwecho.

¹²⁵ Icho ndi choyenera kwa Mkristu aliyense kuti ayime ndi Mawu. Kulondola ndendende. Kuyima ndi Mawu a Mulungu! Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, inu mudzachoka, ine ndidzachoka, mipingo idzachoka, mabungwe adzachoka. Koma Mawu a Mulungu sadzachoka konse! Mukhale okhulupirika, mwendamnjira wokhulupirika!

¹²⁶ Mmasiku a Enoki, chigumula chisanachitike, pamene Enoki ankayang'ana kunja uko ndi kumuwona Nowa akumanga chombocho. Enoki anali mneneri. Enoki ankadziwa kuti iye anali choyimira. Ndipo iye ankadziwa, kuti chigumula chisanafike, kuti iye ankayenera kupereka chitsanzo, chotero masana ena kunali koyenera kwa iye kuti ayende ulendo. Kunali koyenera kuti iye ayende ulendo uwu ndi Mulungu. Ndipo, mwanjira ina, tsiku limenelo iye anasintha njira yake. M'malo mozungulira m'mbali mwa phirilo, iye anatenga Msewuwaukulu wa Amfumu, ndipo anangopitirirabe kumayenda. “Ndipo iwo sanamupezepo iye, chifukwa iye kunalibeko,” koma anayendabe chokwera Msewuwaukulu wa Amfumu!

¹²⁷ O Mulungu, ndiroleni ine ndidzakhale monga Enoki! Pamene oralo lidzafika lakuti ndidzatenge njira, mudirole ine ndidzawupeze Msewuwaukulu wa Amfumu!

¹²⁸ Ine ndikukhoza kumuwona Enoki. Monga iye ankadziwira kuti izo zinali zoyenera kwa iye, pakuti iye anali mneneri, ndipo iye ankadziwa chomwe chikanati chidzachitike. Kotero, ine ndikukhoza kumuwona iye akumupsyopsyona mkazi wake kutsanzikana naye, ndikuti, “Wokonedwa, ndikuwona iwe nthawiyina.” Akuwatenga ana ake, ndipo akuwapsyopsyona iwo potsanzikana nawo; ndipo akupita kwa mwana wake wamwamuna wokwatira ndi mwana wake wamkazi wokwatiwa, ndipo akuwapsyopsyona iwo motsanzikana nawo.

¹²⁹ Iwo anati, “Inu mukupita kuti, abambo? Kodi mukupita kukayenda pang'ono?”

“Inde, ndikupita koyenda.”

¹³⁰ Koma iye sanatenge njira yakale, yodziwikayo tsiku limenelo. Iye anatenga Msewuwaukulu wa Amfumu, ndipo iye

anapitirira ku Ulemelero. Izo zinali zoyenera kwa iye kuti achite zimenezo. Iye sanafune kuti achoke, komabe kunali koyenera kwa iye kuti akwaniritse chirungamo chonse. Chifukwa, iye anali choyimirira cha Mpingo lero. Iye anali choimira cha Mpingo umene uti udzayende ulendo wa kumasana, limodzi la masana awa. Iye tidzakhudzana ndi Msewuwaukulu wa Amfumu, ndipo kutali ife tidzapita!

¹³¹ Eya, kunali koyenera kwa Nowa, kunali koyenera kwa Enoki, kuti iwo akwaniritse chirungamo chonse.

¹³² Ndiye ine ndikufuna kuti ndiyankhule za munthu wina apa. Panali munthu dzina lake Daniele. Ndipo iye anakhala mu tsiku la otsutsa. Inu mukudziwa, Ana a Israeli anali atatengedwa kuchokera ku dziko lakwawo, kupita ku Babeloni, ndipo kumeneko iwo anali okhumudwa, ndipo kwa zaka sevente iwo anali ali kumusi kumeneko. Koma panali mneneri wamng'ono amene anapita kumeneko ndi iwowo, dzina lake Daniele.

¹³³ Ndipo iye ndi gulu laling'ono, abale apang'ono odzadza m'dzanja, anasonkhana pamodzi ndipo anali atalumbirira okha kwa Mulungu, kuti iwo sadzidetsa okha ndi—ndi machitidwe amakono a tsiku limenelo. Iwo anali oti sapusitsidwa ndi nyama za mfumu. Iwo anali oti samamwa zakumwa zawo zaukali. Iwo anali oti samapita nawo ku maphwando ake. Koma iwo anali oti adzisunga okha kukhala oyera ndi odzipereka kwa Mulungu, pakuti potero kunali koyenera kwa iwo!

¹³⁴ Izo zinali zoyenera kwa Daniele, chifukwa iye anali mneneri, mwakuti iye anakhala ndi Mawu.

¹³⁵ Mneneri woona aliyense amene amawadziwa Mawu a Mulungu, amene . . . Ngati iye sakuwadziwa Mawu a Mulungu, ndiye iye si mneneri woona. Mneneri woona amakhala ndi Mawu. Chirichonse chimene Mawu akunena, iwo amakhala kumene ndi Iwo. Ziribe kanthu momwe kachitidwe ka tsikulo kaliri, kapena chimene—mpingo wamakono ukunena, kapena chimene winawake akunena, kapena winawake akuchita chinachakenso, mneneri woona amakhalabe ndi Mawu.

¹³⁶ Ndipo Daniele ankadziwa, kuti ngati iye akhale ndi Mawu, zomwe zikanamuchitikira iye. Izo zikanadzamuchotsera iye kutchuka kwake. Izo zikanadzamuthetsera chiyanjano chake ndi abale ena onse. Izo zikanadzamuchotsera iye zinthu zambiri. Koma iwo anapanga lingaliro, kuti, iwo azipemphera kwa mulungu winawake, kenako pambuyo pake akhoza kubwerera ndi kumakapemphera kwa mulungu aliyense.

¹³⁷ Koma inu mukudziwa, chinachake cha Icho, Mulungu, ife sitimanyengerera pa za Mulungu. Palibepo kunyengere- . . . kunyengerera, ndi Mulungu. Mulungu amangokhala Mulungu basi! Iye samatiyembekezera ife, Lamlungu, kuti tikhale Akhristu, kumamutamanda Iye ndi kumamupembedza Iye; ndipo, Lolemba, awede-wede ndi kuzitsitsira izo pansu,

ndi mitundu yonse ya malingaliro, kuti, “Mwinamwake ine ndimalakwitsa, ndipo ine ndimayenera kuti ndichite *ichi* kapena *icho*.” Ife timakhala okhazikika pa Mawu a Mulungu, ndi kukhala kumene kwa Iwo!

¹³⁸ Chotero ife tikupeza kuti, Daniele, kunali koyenera kwa iye, monga mneneri, kuti ayime ndi Mawu, mulimonsemo! Kotero panali lamulo limene linaperekedwa, ndipo linati, “Kuti aliyense amene adzapembedze mulungu wina aliyense, kupatula mulungu amene iwo anali atamusankha.” Mwa kuyankhula kwina, “Ngati inu simugwirizana ndi ife, ife tidzangokuponyerani inu mu dzenje la mikango.” Chabwino, kunali koyenera kwa Daniele, kunali koyenera kwa iye kuti akwaniritse chirungamo chonse, kuti iye sakapembedza mulungu wina, kapena kudzikola iyemwini ndi dziko lapansi; koma kwa Mulungu yekha basi! Kotero, iye anangotsegula mazenerawo ndi kusunthira mmwamba zimango zake, ndipo anatsegula makataniwo, ndi kuyang’ana kunjira cha Kummawa, ndi kumapemphera katatu pa tsiku, basi monga momwe amachitira nthawizonse. Chifukwa chiyani? Osati kuzembera kwinakwake ndi kukabisala, kuti achite zimenezo, koma iye ankatsegula mazenera; ndi kulola aliyense kuti aziwona, amene angafune kutero. Iye sankachita manyazi ndi chipembedzo chake.

¹³⁹ Chifukwa, ndi zoyenera kwa Mkhristu kusachita manyazi ndi chipembedzo chako. Monga Paulo, wakale, ananena, “Munjira imene imatchedwa mpatuko, yamisala, imeneyo ndi njiya imene ine ndimapembedzera Mulungu wa makolo athu.” Mukuona? “Ine sindimachita manyazi ndi Uthenga wa Yesu Khristu,” iye anati, “pakuti ndi Mphamvu ya Mulungu kwa chipulumutso, kwa aliyense amene amakhulupirira Iwo.” Uko nkulondola, osachita nawo manyazi Uthenga! Ndicho chinthu chimene chimagwira m’maora amene ngalawayo ikugwedezeza ndipo nyenyezi iliyonse siyikuwoneka, ndipo mwezi ndi nyenyezi, ndi mikuntho ikuwomba. Icho chimagwirabe, pakuti ndi Uthenga wa Yesu Khristu!

Daniele anali wokhulupirika. Izo zinali zokakamizika kwa iye.

¹⁴⁰ Ana Achihebri, chinali chokakamizika kwa iwo, chowayenera iwo, iwo atatha kupanga mayimidwe awo kwa Mulungu. Izo zinali zoyenera kwa iwo. Iwo sanasamale za ng’anjo yamoto. Pansi pa mayeso ovuta, kodi iwo anasamala chiyani? Iwo anali atapanga mayimidwe!

¹⁴¹ O Mulungu, ngati Akhristu a lero atangochiwona chimenecho! “Ine nditenga njira yanga ndi onyozeka ochepa a Ambuye. Ine ndayamba ndi Yesu, O Ambuye, nditengeni, ndipyoletseni ine.” Pansi pa yesero, zovuta, zopweteketsa mtima, imfa, matenda, chisoni, ine ndidzaponyabe maere anga

pa Yesu Khristu, kudzatenga maimidwe anga! “Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndayima, maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.” China chirichonse chikumira. Maufumu adzagwa, ndipo mafuko adzasweka, ndipo zipembedzo zidzabalalika, ndipo afioloje adzafa, koma Mawu a Mulungu, adzakhalabe chimodzimodzi!

¹⁴² Inde, kunali koyenera kwa iwo kuti atenge mayimidwe awo. Ndipo kunali koyenera kwa iwo, atatha kutenga mayimidwe, kuti iwo anakhalabe pa mayimidwe awowo.

¹⁴³ Pamene muzibwera mmawa uno, mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu, ndipo inu nkutenga mayimidwe anu, zikuyenera kwa inu kuti musachitire umboni chirichonse chotsutsana ndi chimenecho; kapena, musabwere. Uko nkulondola. Ngati simukumverera kuti Mulungu akuchizani inu, ndiye mukhale kutali, inu mukungochita chipongwe pa izo.

¹⁴⁴ Ngati mukumverera, mmawa uno pamene kuyitanira paguwa kubwera, kuti, “Ine ndikufuna kutenga mayimidwe anga kwa Khristu.” Ngati inu mukumverera, muwerenge mtengowo; muwerenge amuna anu, muwone ngati mungakwanitse kupita ku nkondo. Muwone ngati ndinu okonzeka. Ngati simukumverera kuti mwakonzeka, musati mubwere. Koma ngati Chinachake chikukuuzani inu, “Ili ndi tsiku langa, uwu ndi m’*mawa wanga*,” ndiye inu mubwere ndi kudzakhazikika pamenepo! Musati musunthe nkomwe, ziribe kanthu ngati imfa ingakuyang’aneni inu, ndipo chifunga nkumayandama pa nkhope yanu. Kodi inu musamala chiyani? Imani pamenepo! Pakuti, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita; Mawu Anga sadzalephera konse!” Inu mudzakhala ndi Iwo.

¹⁴⁵ Pamene inu mukuti, “Ndikumukhulupirira Yesu Khristu ngati Mchiritsi wanga. Ine ndikukhulupirira, mmawa uno, kuti Iye achiza thupi langa lodwala. Chinachake chinandiuzza ine kuti ndibwere ku tchalitchi. Ine ndiri pano pakati pa okhulupirira. Ine ndikutenga kuyima kwanga, mmawa uno. Ine ndikukhulupirira Izo! Ine ndikupita kuti ndikapemphereredwe. Pamene ine ndipemphereredwa, pamenepo pa mayimidwe amenewo ine ndidzaimabe! Ziribe kanthu momwe kungakhalire kwa mdima, kapena kumene izo ziri, ine ndidzayimabe pa mayimidwe amenewo.” Inu munatenga mayimidwewo chifukwa ndichoyenera kwa inu.

¹⁴⁶ Inu mutatha kupanga kuvomereza kamodzi, mukuyenera kuyima ndi kuvomereza kwanuko. Izo nzoona. Izo zikukukakamizani inu, monga Mkhristu, monga wokhulupirira, kuti mukhale ndi mayimidwe anowo.

¹⁴⁷ Musamamulole mdierekezi azikukankhirani inu *apa* ndi *apo*. Nthawizonse inu mumakhumudwa. Inu nthawizonse mumachoka panjira yeniyeniyo. Inu nthawizonse mumalowa ndi kutuluka. Ndipo ndi momwe inu simumakhazikika paliponsepo.

Inu simungakhale ndi chidaliro mwa inumwini. Kapena, inu simungathe, palibe amene angakhale ndi chidaliro mwa inu. Inu mukuyenera kuyima! Ndipo pamene inu mwachita zonse zomwe mungathe kuti muyime, ndiye imani! Muzingopitirira kumayima! Uko nkulondola. Ife tiyenera tizichita zimenezo. Izo ndizoyenera kwa ife. Izo ndizokakamizika kwa ife, kuti tizichita zimenezo.

¹⁴⁸ Izo zinali zokakamizika kwa Eliya, zoyenera kwa Eliya mneneri, mwakuti iye anapanga kuyima kwake kuti akwaniritse Mawu a Mulungu, chifukwa iye ankawadziwa Mawu a Mulungu. Ndipo iye ankadziwa kuti arkibishopu uyu, Yezebeli, ndi kutsemphana kwawo konse kwa zipembedzo kunkagwirizana ndi kachitidwe ka dzikolo. Zinali zoyenera kwa Eliya, monga mneneri, mwakuti iye anayima. Ndipo iye anayima yekha! Anati kwa Mulungu, “Iwo onse apita, koma ine, ndayima ndekha.” Umo ndi mochulukwa momwe iye ankadziwira. Mulungu anati Iye anali ndi enanso amene anali atatenga kayimidwe komweko; mwinamwake osati pamalo amene—amene Eliya anali, chifukwa iye anali chandamale kwa fukolo. Iwo sankakumana ndi kutsutsidwa monga iye ankachitira, chifukwa iwo onse anali akuwombera molunjika pa iye, chifukwa iye anali mneneri. Koma kunali koyenera kwa iye, mkatikati mwa yesero, mkatikati mwa kutsutsidwa, mkatikati mwa kusayanjanitsika; kunali koyenera kwa Eliya, monga mneneri, kuti atenge mayimidwe ake pa Mulungu, ndi kuyima pamenepo.

¹⁴⁹ Ndichotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Amuna aakulu, amphamvu, akuchitira mthunzi tsiku lino pamene zipembedzo za Yezebeli ndi zinthu zikuwuka tsopano, zinthu zimene ife tiri nazo lero, zikuyesera kuti zitenge malo. Ndichoyenera kwa wantchito wa Mulungu, ziribe kanthu chimene aliyense akunena kapena chimene chingachitike, imanibe, chifukwa ndi chotiyenera kuti ife tikhale ndi Mawu.

¹⁵⁰ Eliya ankadziwa kuti iye anali mneneri. Iye ankawona masomphenya. Mulungu anali atamutsimikizira iye kukhala mneneri. Kotero zinalibe kanthu ngati abale ake. . . Analipo mateni amasauzande; tangoyang’anani pa a Israeli, mamillioni a iwo, anthu amene ankadzinenera kuti ankakhulupirira mwa Yehova, iwo anali—iwo anali atadzipanga okha bungwe. Iwo anali atasandulika kukhala amakono, monga momwe iwo aliri lero. Iwo anasandulika kukhala amakono. Iwo analekerera pa Mawu Ake. Aleluya, koma kunali koyenera kwa iye, Eliya, kuti akwaniritse chirungamo chonse. Kotero iye anayima pamenepo, yekha, akufuula motsutsa zoyipazo! Ngati iwo akanatenga moyo wake, nanga bwanji za iwo? Kunali koyenera kwa iye, kuti akwaniritse chirungamo chonse. Munali choyipa mdzikolo. Munali kusayanjanitsika mdzikolo. Munali zolakwika za Mwamalemba mdzikolo. Ndipo kunali koyenera kwa Eliya, kuti akwaniritse chirungamo chonse, kuti amuimirire Yehova;

kenako Yehova anamuimirira Eliya. Ameni. Ndichoyenera kwa iye!

¹⁵¹ Abrahamu. Izo zinali zoyenera kwa Abrahamu kuti adzilekanitse yekha ku kusakhulupirira. Ndichoyenera kwa wokhulupirira aliyense kuti mudzilekanitse nokha ku kusakhulupirira! Abrahamu, chinali choyenera kwa iye kuti ayende mdziko lakelake, iye ndi Mulungu, yekha, chifukwa iye anali mneneri. Dziko silinamvetse chifukwa chimene Abrahamu anapangira chisankho choterocho. Nchifukwa chiyani iye anachoka kwawo? Nchifukwa chiyani iye anasiya tchalitchi chake? Nchifukwa chiyani iye anawasiya anthu ake? Nchifukwa chiyani iye anachita chinthu chopupuluma chomwecho, kukayenda mdziko lachilendo limene kunalibe madzi kapena chakudya? Nchifukwa chiyani iye anapita m'zipululu zopanda zomera zimenezo kumene anthu anali asanapiteko? Koma zinali zoyenera kwa iye, pakuti iye anali mneneri, kuti adzilekanitse yekha ku kusakhulupirira konse, ndi kuti akayende yekha ndi Mulungu. Mulungu anati, “Dzilekanitse wekha, ndipo Ine ndidzakudalitsa iwe.”

¹⁵² Pamene udzipatula wekha ku kusakhulupirira konse, Mulungu amakudalitsa iwe. Ndipo ndichoyenera kwa aliyense wa ife, mosalabadira mtengo wake, kuti tidzilekanitse tokha ku dziko losakhulupirira. “Tulukani pakati pawo, ndipo mukhale odzilekanitsa,” atero Mulungu, “Ine ndidzakulandirani inu.” Ndi choyenera kwa ife, monga amuna ndi akazi a Mulungu, kuti titenge mayimidwe athu mu ora la mdima ili limene ife tikukhalamo.

¹⁵³ Abrahamu, mosalabadira zomwe ena onsewo ankaganiza, iye anadzilekanitsa yekha. Chifukwa chiyani? Iye anali atamuwona Mulungu. Iye anawona masomphenya. Masomphenyawo anali owona, masomphenyawo anafika podzachitika. Iye ankadziwa kuti Mulungu anali ndi iyeyo; Abrahamu, kuti apange neno lopupuluma monga iye anachitira. Mwamuna wa zaka handirede, ndi mkazi wa zaka nainte, ndipo mkaziyo anali wowuma ndipo mwamunayo anali wosabala, ndipo iwo anali oti akakhala ndi mwana pa usinkhu uwu. Bwanji, sayansi ya zamankhwala ya tsiku limenelo ikanamutcha iye mtundu wina wa wosamvetsetseka. Iwo akanamutcha iye “wamisala.” Koma chinali chowayenera. Aleluya!

¹⁵⁴ Nthawizina zimakhala zoyenera kukhala wosamvetsetseka, ngati izo ziri molingana ndi Mawu.

Mulungu anali atayankhula ndi iye, anati, “Abrahamu.”

Anati, “Inde, Ambuye?”

¹⁵⁵ “Ine ndine Mulungu wa makolo anu. Ine ndine Mulungu wa Muyaya. Ine ndine El Shaddai; Ine ndine Chifuwa, Ine ndine Bere, Ine ndine Wopereka-Mphamvu. Ine sindikusamala kuti iwe uli ndi zaka zingati, Abrahamu, zimenezo ndi chiyani kwa Ine?”

Ine sindikusamala momwe iwe uliri wosabereka kapena kuti chiberekero chake ndi chowuma bwanji, Ine ndidzakupatsa iwe mwana wamwamuna.”

Ndipo Abrahamu anati, “Ine ndikukukhulupirani Inu, Mulungu.” Aleluya!

¹⁵⁶ Baibulo linati, “Iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu, mwa kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu.” Chifukwa chiyani? Zinali zoyenera kwa iye. Iye anali atawona dzanja la Mulungu likusuntha, mu mphamvu.

¹⁵⁷ Oh, Branham Tabernacle, kodi ndi mawu a mtundu wANJI amene ife titi tidzawapereke pa Tsiku la Chiweruzo? Pamene, ife tawona dzanja Lake lamphamvu. Ife tawona Mphamvu Yake. Ife tawuwona Ulemelero Wake. Ife tawona zomwe Iye ananena; Izo sizimalephera konse. Ife tawuwona Umunthu Wake, Lawi la Moto lalikulu, Kuwala kutapachikika mchipinda muno. Ife takuwona Iko uko, sayansi yajambula zithunzi za Iko, ndi chirichonse. Ndi kuwumva Uthenga ukupita, molunjika kumene pa mzere, “Dzilekanitseni nokha kwa iwo! Musayanjane ndi chirichonse cha kusakhulupirira!” Ndichoyenera kwa ife, kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

¹⁵⁸ Abrahamu anadzinenera kuti iye anali mwendamnjira ndi mlendo. Iye analibe chochita chirichonse; iye sankamudziwa aliyense pa dziko lapansi. Iye ankayenda ndi Mulungu, chifukwa chinali choyenera kwa iye, chifukwa anali atamuwona Iye. Icho chinali choyenera kwa Abrahamu. Pamene mafumu onse awo anakomana kunja uko, inu mukudziwa, kuti akamupange iye kukhala munthu wamkulu kwambiri; mafumu onse, Abrahamu atatha kupeza chigonjetso chachikulu ichi, pamene mafumu anakomana ndi iye kunja uko, abale onse achipembedzo, ndipo anati, “Iwe ukudziwa, Abrahamu, ife ti—ife tipanga mgwirizano ndi iwe. Ife tichita *chakuti-ndi-chakuti*.”

¹⁵⁹ Iye anati, “Ine sinditenga ngakhale chingwe cha nsapato, kwa ine; kuwopa mungadzanene kuti, ‘Ine ndinampanga Abrahamu kanthu.’”

¹⁶⁰ Oh, zinali zoyenera kwa iye, pakuti iye ankadziwa (Aleluya) kuti Mulungu analumbirira kwa iye, “Ine ndikupatsa iwe kulikonse kumene ungayang’ane: kummawa, kumpoto, kumadzulo, kapena kummwera.”

¹⁶¹ Zimapanga kusiyana kotani ngati ife tiri ndi faivi tambala kapena twente tambala, kaya ife tiri ndi chinachake choti tidye kapena ife tiribe, kaya ife tikukhala moyo kapena tikufa? Mulungu analonjeza, “Ofatsa adzalandira dziko lapansi.” Izo ndizotikakamiza ife, ndizoyenera kwa ife, kuti ife tidzikhala monga chomwecho, kumachita monga chomwecho, tiyenera kukwaniritisa chirungamo chonse. Mulungu akufuna amuna ndi

akazi amene adzayime ndi kukwaniritsa chirungamo chonse! Zoonadi, *chirungamo* ndi “Mawu Ake.”

¹⁶² Monga ndinanenera kumayambiro kwa ulaliki, icho ndi chifukwa chake chimene Yesu anabatizidwira. Zinalibe kanthu momwe izo zinaliri. . . Ngati Iye ankadzinenera kuti anali Mwana wa Mulungu, ndiye nkubatizidwa, kuloza ku chikhululukiro cha machimo? Iye analibe aliwonse. Koma Iye ankayenera kuti atsukidwe, chifukwa Iye anali Wansembe Wamkulu. Iye ankayenera kukwaniritsa chirungamo chonse. Anati, “Balola izo, Yohane. Ine ndikudziwa kuti iwe ukudziwa zimenezo. Ine ndikudziwa kuti ndikudziwa zimenezo. Ndipo ife tikudziwana wina ndi mzake. Koma ife tilole kuti izo zikhale chomwecho, koma izo ndi zoyenera kwa ife.” Ameni! Aleluya!

¹⁶³ Ndiye ine ndidzatenga njira ndi onyozeka apang’ono a Ambuye! Ndizoyenera kwa ine, ndizoyenera kwa inu, monga antchito a Mulungu, kuti titenge njira ndi onyozeka apang’ono a Ambuye; kuti tiziyenda mwaumulungu, molungama, moyera, mmoyo wapakali panowu; kusiya pambali cholemetsa chirichonse chimene sichimachedwa kutifooketsa ife; kuyang’ana kwa Woyambitsa ndi Wotsirizitsa wa chikhulupiriro chathu, Yesu Khristu! Ameni.

Izo zinali zoyenera kwa Abrahamu, pamene iye ankayenda kupita kumeneko.

¹⁶⁴ Ndipo Mulungu anamuza iye, “Tsopano, umutenge mnyamata wamng’ono uyu. Tsopano ndiwe wa usinkhu wa zaka handirede ndi (pafupifupi) twente zakubadwa. Ndipo iwe uli ndi mnyamata wamng’ono pano, wamutu waung’ono wa mzindo. Iye ndi kanthu kakang’ono kokoma. Koma ine ndikufuna kuti iwe umutengere iye pamwamba pa phiri apo, ndi ukampereka iye nsembe, mwa iye Ine ndidzapanga mafuko ambiri kuchokera mwa iwe.” Izo zikanatheka bwanji? Zinkawoneka ngati Mulungu anali atasokonezeka. “Ine ndidzatenga, kupyolera mwa Isaki, ndi kudzadalitsa dziko lonse ndi fuko lililonse, ndi iye; koma Ine ndikufuna iwe, kuti umutengere iye, pamwamba apo ndipo ukamuphe iye. Kudzera mwa mbewu ya Isaki. . .” Aleluya! “Kudzera mu Mbewu ya Isaki Ine ndidzadalitsa fuko lililonse pansu pa Miyamba, koma Ine ndikufuna kuti iwe umutengere iye kumeneko ndipo ukamuphe iye.”

¹⁶⁵ Oh, bambo wokhwima, wolimba, wokalamba ameneyo; ali ndi nkhu ni ndi thumba pa nsana pake, akumutsogolera bulu. Mai! Isaki wamng’ono akuyenda patsogolo pa iye! “Iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu, kupyolera mu kusakhulupirira.” Zinali zoyenera kwa iye!

¹⁶⁶ Pakuti Abrahamu anati, iyemwini, “Ndinamulandira iye monga mmodzi wochokera kwa akufa, ndipo ndine wokopedwa kwathunthu kuti Mulungu ndi wokhoza kumuukitsa Iye kenanso.” Ameni! Kunali koyenera kwa Abrahamu, kuti

akwaniritse chirungamo chonse. Iye ankadziwa chimene iye ankachikamba. Iye ankamudziwa Mulungu wake. Iye anadziwa, kuti chimene Mulungu ananena, Mulungu anali wothekera kuchichita. Lonjezo limene Mulungu analipanga, Mulungu ndi wokhoza kusunga lonjezo Lake, mulimonsemo. Kotero, kunali koyenera kwa Abrahamu kuti akwaniritse chirungamo chonse.

¹⁶⁷ Kunali koyenera kwa ophunzira, pa Pentekoste, kuti apite ku chipinda chapamwamba chiya. Chifukwa chiyani? Nchifukwa chiyani kunali koyenera? Chifukwa iwo anali atakumana ndi Munthuyo; Kalipentara, wodziwika ku dziko, Mlendo waku Galileya wa dzina loyipa, “wapathengo.” Koma iwo anali atamuwona Munthu ameneyo akuwukitsa akufa. Iwo anali atamuwona Munthu ameneyo akutsegula maso akhungu. Iwo anali atamumva Munthu ameneyo akulalikira Mawu osaipitsidwa, a Mulungu. Ndipo iwo ankadziwa kuti Iye anali Mesiya. Iwo anali atawona zizindikiro zonse pomuzungulira Iye. Iwo anali atamumva Mulungu akuyankhula kuchokera Mmiyamba. Iwo anali ataliwona Lawi la Moto lija litapachikika pa Iye. Iwo anadziwa kuti Iye anali Mesiya. Ndipo pamene Iye anawauza iwo, “Ndi koyenera kwa Ine kuti ndichoke; koma Ine ndikufuna inu mupite kumeneko ku mzinda wa Yerusalemu, ndi kukakhala kumeneko. Mukangodikirira kumeneko.”

“Motalika bwanji?”

“Mpakana!”

“Izo zidzakhala nthawi yayitali bwanji, Ambuye?”

¹⁶⁸ “Basi mpakana! Mpaka mutadzazazidwa ndi Mphamvu yochokera Kumwamba! Mukadzatero mudzakhala mboni Zanga.”

“Izo zikakhala nthawi yayitali bwanji, Ambuye?”

¹⁶⁹ “Kwa m’badwo *uno*, ndi kwa m’badwo *uwo*, ndi onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana. Ku Yerusalemu, Yudeya, Samariya, ndi kumalekezero a dziko lapansi. Koma, inu musanapite, Ine ndikufuna kuti mukadikirire! Ine ndikakuchitirani inu chinachake.”

¹⁷⁰ Kunali koyenera kwa iwo kuti anapita mchipinda chapamwamba, chifukwa iwo anali atawona Mphamvu Yake. Iwo anadziwa kuti Iye anafa, wakufa. Anafa kufa kwenikweni mwakuti ngakhale mwezi ndi nyenyezi zinachitira umboni kuti Iye anafa, izo zinabisa nkhope zawo ndipo sizikanakhoza kuwala. Dziko lapansi linadziwa kuti Iye anali atafa, mpaka ilo linagwedezeka ndi kudzilambatitsa kwamanjenje. Miyala inageya kuchokera pansu, imene inali itakhala mmenemo kuyambira pa chiwonongeko cha chigumula. Iwo anadziwa kuti ameneyo anali Mesiya. Iwo anadziwa kuti, Mawu Ake anali, kuti Iye anali woti adzatumizenso Mzimu Woyera. Iwo anadziwa kuti ilo linali lonjezo. Iwo ankadziwa kuti iwo ankayenera kuti akadikirire Iwo kumeneko. Iwo anali atamuwona Iye.

Iwo anadziwa kuti Iye anali atafa; iwo anadziwa kuti Iye anali atauka. Iwo anali atamuwona Iye, chotero iwo anadziwa chimene iwo anali kuchikamba.

¹⁷¹ Kufikira munthu atadziwa chimene akuchikamba, iye sangathe kunena zochuluka. Koma pamene iwe ukudziwa zomwe ukuzikambazo! Ngati mukuganiza kuti uku ndi kutengeka, bwerani mudzakupeze Iko kamodzi, ndiye mudzadziwa chimene mukuchikambacho. Iko si kutengeka. Ndi Mphamvu ya Mulungu kwa chipulumutso. Ndi Mzimu Woyera. Ndikudziwa chimene ndikuchikamba. Aliyense, amene anamulandira Iye, amadziwa chimene iwo amayankhula.

¹⁷² Kunali koyenera kwa ophunzirawo, kunali kowayenera iwo kuti asunge Mawu Ake, kuti akadikirire ku Yerusalemu. Kotero iwo anapita uko kuti akadikirire pa Pentekoste, kufikira atalandira Mzimu Woyera. Pakuti, potero iwo anadziwa kuti utumiki wawo sukanakhoza kupitirira mpaka iwo atalandira Mzimu Woyera, kuti uchitire umboni za Iye. Iwo ankadziwa kuti iwo anali opanda thandizo. Koma iwo ankayenera kukhala ndi Kukhalapo Kwake, kotero iwo anapita kukadikirira pa Iwo.

Zinali zokakamizika kwa Petro, Yesu atatha kukumana naye iye.

¹⁷³ Mu Marko 16, anati, “Pitani mu dziko lonse lapansi, ndipo mukalalikire Uthenga. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda, adzayankhula ndi malirime atsopano, adzatenga njoka; adzamwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo; ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.”

¹⁷⁴ Kunali koyenera kwa Petro Woyera, nsodzi wakaleyo, analibe maphunziro okwanira kuti alembe dzina lake lomwe. Koma tsiku lina pamene iye ankadutsa pa chipata Chokongola chimene Solomoni anali atachimanga, pamenepo panali munthu amene anali wolumala. Mawondo ake anali ofooka, polumikizira chidendene, iye samatha kuyenda. Iye anali atakhala mwanjira imeneyo. Iye analibe mphamvu. Bambo wa zaka pafupifupi forte, ndipo iye analibe mphamvu. Koma pamene Petro anamva chikho chikupanga phokoso, ndipo iye anayang’ana pansi ndipo anawona munthu wolumala atakhala pamenepo, ndipo Chinachake chinagunda mu mtima mwake! Iye anakhala ali pa Pentekoste, iye anali ndi Mzimu Woyera! Iye anali ndi lonjezo la Yesu, kotero kunali kokakamizika, kunali koyenera kwa iye, mwakuti iye anati, “Siliva ndi golide ine ndiribe.” Iye anapereka umboni wake, “Ine ndiribe siliva ndi golide. Koma, chimene ine ndiri nacho, ine ndipereka icho kwa iwe ngati iwe ungathe kuchilandira icho.”

Ndikukhoza kulingalira munthuyo akunena kuti, “Ndikhoza kulandira icho.”

¹⁷⁵ Anati, “Ndiye, mu Dzina la Yesu Khristu waku Nazareti, imirira pa mapazi ako ndipo uchiritsidwe.” Ndipo iye anafikira pansi ndi kukamugwira iye, kuwonetsera chikhulupiriro chake, ndipo anamudzutsa iye monga choncho; ndipo mafupa ake apolumikizira chidendene analandira mphamvu, ndipo iye anapita, akutsimphina, akutamanda ndi kumulemekeza Mulungu.

¹⁷⁶ Izo zinali zokakamizika kwa iye kuti achite zimenezo, izo zinali zoyenera kwa iye. Iye ankayenera kuchita zimenezo, chifukwa iye anali wophunzira wodzozedwa. Iye anali atakhala ndi Yesu. Dziko lapansi lonse linadziwa, dzulo lake, mu Bwalo lamilandu la Sanhedrin, pamene iwo anamusonkhanira iye, iyeyo ndi Yohane, awiri onse a iwo, mbuli ndi osaphunzira; iwo anadziwa kuti iwo anali atakhala ndi Yesu, chifukwa iwo anamva momwe iwo ankayankhulira, kulimba mtima kumene iwo anali nako. Iwo anadziwa kuti chinachake chinali chitawachitikira iwo. Ndipo Petro amadziwa zimenezo. Kotero izo zinali zoyenera kwa Petro, izo zinali zoyenera kwa iye chifukwa iye anali ndi lonjezo la Mulungu la tsiku limenelo.

¹⁷⁷ “Ine ndidzakupatsani inu Mphamvu.” Hmm! “Ine ndidzakupatsani inu Mphamvu. Inu muzidzaponda pa mitu ya njoka ndi zinkhanira. Chirichonse chimene mudzapempha mu Dzina Langa, chimenecho Ine ndidzachichita. Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Sunthidwa,’ ndipo osakaikira izo mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti chimene mwanenacho chichitika, inu mukhoza kudzakhala nacho chimene mwanenacho.”

¹⁷⁸ Zinali zoyenera kwa Petro nthawi imeneyo kuti akhulupirire Zimenezo, zinali zomuyenera iye, icho ndi chimene iye ankayenera kuchita, chifukwa iye ankadziwa kuti iye ankakhala mu tsiku la kutuma kumeneko. Uko kunali Kuwala kwa oralo. Chiukitsiro chinali chitangobwera kumene, Mzimu Woyera unali pamenepo. Izo zinali zoyenera kwa iye.

¹⁷⁹ Izo zinali zoyenera kwa Paulo Woyera, atatha kukhala wotsutsa. Ndipo ali pa ulendo wake waku Damasiko tsiku lina, kumeneko Lawi la Moto lija limene linatsogolera Israeli kuchokera ku Igupto kupita ku dziko lolonjezedwa, limene linali litasandulika thupi ndipo linadzakhala pakati pawo ndipo linabwereranso kwa Mulungu, linayankhula kwa iye. Ndipo iye anadabwa, “Kodi zingatheke bwanji Uyu kukhala Yehova? Kodi zingatheke bwanji? Ndipo pamenepo Iye ali mu Lawi la Moto lomwelo, litapachikika pamenepo. Ambuye, Inu ndinu yani amene ine ndikumuzunza?”

¹⁸⁰ Iye anati, “Ine ndine Yesu.” Oh, mai! Iye anamutuma iye, anamupatsa iye utumiki wake. Anamutuma Paulo, anamupatsa iye utumiki wake.

¹⁸¹ Paulo anali atakhala mu Kukhalapo kwa Mulungu, iye anali atawona Lawi la Moto. Iye anamuwona Yesu ameneyo amene nthawiyina anali Lawi la Moto, kenako anadzasantulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu, ndipo anabwereranso ku Lawi la Moto, ndipo anamutuma iye ku utumiki wake. Aleluya! Palibe chimene chikanati chidzamugwedeze iye. Kunali koyenera kwa iye, pamene iwo anachotsa mipango pa thupi lake ndipo anayitumiza kwa odwala. Izo zinali zoyenera kwa iye, chifukwa iye ankadziwa kuti iye anali mtumwi wodzozedwayo. Ankawona masomphenya a Mulungu, ndipo Mulungu amawonekera pamaso pake ndipo ankayankhula, ndipo amaziwona izo zikuchitika ndendende basi. Bwanji, izo zinali zoyenera kwa Paulo, pamene iye ankayesetsa kuti awathandizire anthu, pokwaniritsa Mawu amene iye anatumidwa. Iye anali Kuwala kwa tsikulo. Iye anali Kuwala kwa Amitundu. Iye ankadziwa zimenezo. Mulungu anamutuma iye kuti adzakhale. Iye anali Kuwala mu tsiku limenelo. Koteru, Iye anatumidwa kwa Paulo.

¹⁸² Tsopano izo ndizoyenera kwa ife, ndizotiyenera ife mu tsiku lino. Ife tikudziwa! Ife tangodutsa kumene Mibadwo ya Mpingo. Ife tikudziwa kuti ife talandira Mzimu Woyera, ife tikudziwa zimenezo mopanda mthunzi wa kukayikira. Ife tikudziwa kuti tiri nako Kuwala kwa Uthenga.

¹⁸³ “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Mulibe mlaliki mdziko, kapena china chirichonse, amene angakane Iwo. Kodi izi zikuyenera zichitike mpakana kuti? “Lonjezo liri kwa ana anu, kwa iwo amene ali kutali, ngakhale ochuluka amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.”

¹⁸⁴ Mneneri anati, “Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo, Kuwala kwa Uthenga uku kukanadzabwereranso.” Monga dzuwa lomwelo limatulukira Kumwawa ndi kukalowa Kumadzulo, Ilo likanadzabwereranso mmasiku otsiriza. Ndi ife pano mmasiku otsiriza!

¹⁸⁵ Ife talandira Mzimu Woyera. Ife tikudziwa zimenezo. Ife tinayankhula mmalirime monga iwo anachitira pa Pentekoste. Ndipo ife tikudziwa kuti inu mukhoza kulandira Iwo.

¹⁸⁶ Ife tikudziwa kuti mngelo wachisanu ndi chiwiri wapereka Uthenga. Ife tikuwuwona Iwo ukutsimikiziridwa, chizindikiro.

¹⁸⁷ Ife tikudziwa kuti tiri pa mapeto a M’badwo wa Laodikaya. Ife tikudziwa kuti mikangano ya fuko, zizindikiro ndi zodabwitsa, zikuwonekera konsekonse. Ife tikudziwa kuti tiri ku mapeto a nthawi.

¹⁸⁸ Mulungu akuchitira umboni! Ndipo izo zikutikakamiza ife, izo ndi zoyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse. “Mafuko kuwukirana ndi mafuko, kupsyinjika pa

nthawi, osautsika,” zinthu zonsezi zimene ife tazimva. Ngati inu mungathe kuwulandira Iwo!

¹⁸⁹ Tsopano ife tiri pa ora lotsiriza. Ife tiri mu M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Mtumiki aliyense wapereka m’badwo wake, wapereka Uthenga wake mu m’badwo wake. Ndipo ife tiri pano pa mapeto a m’badwo, ndipo ife tikuwona kuti Mulungu watsimikizira izo ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Ndipo palibe amene anganene kuti izo siziri chomwecho.

¹⁹⁰ Iye ali pano tsopano! Iye ali mu Mpingo! Iye ali mwa anthu. Palibe amene anganene kuti izo siziri chomwecho. Ife tikudziwa kuti Iye ali pano.

¹⁹¹ Ndipo izo zikutikakamiza ife kuti titenge Mawu Ake. Ife, izo zikutikakamiza ife kukhulupirira chirungamo chonse. Izo ndi zotikakamiza ife. Ndizotiyenera ife kuti tikwaniritse chirichonse chimene Iye wayankhula.

¹⁹² Mpingo ndi wofooka, mipingo ya lero. Ife tasweka mu ndewu za bungwe, kulekana kwa ubale; Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Aumodzi, Autatu, Ausanu, mitundu yonse ya zinthu. Ife tasweka. Umo ndi momwe izo zikuyenera kukhalira. Izo zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo.

¹⁹³ Zikadzatero padzabwera Uthenga! Oh, Aleluya! Ife tikudziwa kuti ndi Lawi la Moto lomwelo limene linatsogolera Israeli. Ife tikudziwa kuti utumiki womwewo umene unamuperekeza Yesu Khristu, mwa Lawi la Moto limenelo limene linamudzoza Iye, likuperekeza Mpingo lero. Sayansi yatsimikizira zimenezo; ife sitikusisowa zimenezo. Mulungu watsimikizira zimenezo! Ife tikusowekera utumiki wa Yesu Khristu kuti udzakwanirane ndi Mwalawapamutu umenewo umene ukubwera kumeneko, umene wawubweretsa Mpingo mu malo amene utumikiwo uli chimodzimodzi monga momwe unaliri pamene Yesu ankachoka. Ndendende!

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,
Zizindikiro zimene aluntha ananeneratu;
Masiku a Amitundu akutha, ndi zowawa
zochuluka;
“Bwererani, O omwazikana, kwanu komwe.”

¹⁹⁴ Ife tiri mmasiku otsiriza. Ndipo ndizotikakamiza ife, ndi koyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

¹⁹⁵ Kumbukirani, Yesu anati, “Monga izo zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Ndi angati akukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino. Kodi chinali chiyani mmasiku a Loti? Kodi Iye anapereka chizindikiro chotani?

¹⁹⁶ Kunali magulu atatu a anthu mmasiku a Loti. Kodi izo zinali zolondola? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kunali wosakhulupirira, wodzipangitsa-kukhulupirira, ndi

wokhulupirira. Aliyense wa iwo analandira wamthenga. Uko nkulondola. Pamene Abrahamu anali atakhala pansu pa thundu wake, chinachitika ndi chiyani? Taonani chimene chinachitika.

¹⁹⁷ Pamenepo panali Mngelo amene anatsikira pansu ndipo anapita kumusi mu Sodomu. Munthu uyu anapita kumusi kumeneko ndipo anakaphunzitsa kulapa kwa iwo, kuti iwo ayenera alape ndi kutembenukira kwa Mulungu. Chinachitika ndi chiyani? Atatu okha anatuluka, Loti ndi ana ake aakazi awiri. Mkazi wake anasanduka chulu cha mchere. Atatu okha anatuluka, pamene kunali Billy Graham wamakono amene anawombera uthenga kumeneko kwa iwo.

¹⁹⁸ Ndipo ife tikuziwona izo zikuchitika lero. Ife tikuwona, kwa mpingo mwa dzina lokha, ife tikuwona mtumiki akupita, akulalikira.

¹⁹⁹ Ndipo panali Mmodzi Amene anabwera kwa Abrahamu ndi Mpingo wosankhidwa. Iye anawapatsa iwo chizindikiro. Ndipo ife tikudziwa kuti izo ndi zooni. Iye tikudziwa kuti ndi zooni. Iye anakhala atatembenezira nsana Wake ku hema, ananena chimene Sarah anali, chimene chinali pa mtima pake, chimene chinali vuto lake. Iye anapereka uthenga, ndendende. Abrahamu anadziwa kuti ameneyo anali Mulungu. Pakuti, mwamsanga Iye atanena chomwecho, iye anamutcha Iye, “Elohim,” Wamthenga, atawumbidwa nu thupi la munthu, kuti akabweretse Uthenga ku Sodomu ndi Gomora.

²⁰⁰ Ndipo pamene ife tiziwona zinthu zimenezo zimene Yesu ananena kuti zikanadzachitika, ndi koyenera kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Ndi koyenera kwa ife kuti timutenge Mulungu pa Mawu Ake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Balola kuti izo zikhale chomwecho tsopano.

²⁰¹ “M’bale Branham, ndinu—ndinu—inu mwasokonezeka ndi onsewo, zipembedzozo.”

²⁰² Izo zikhoza kukhala chomwecho. Balolani kuti izo zikhale chomwecho tsopano. Uko nkulondola, balolani kuti izo zikhale chomwecho.

²⁰³ “Chabwino, zikanakuchitirani bwino kwambiri ngati mukanapitirira ndi kukachita mogwirizana.”

²⁰⁴ Balolani kuti izo zikhale chomwecho tsopano, zimenezo. Koma kotero izo ndizotiyenera ife. Ife ndi anthu Ake, aneneri Ake, anzeru Ake. Ndizotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Kotero, tiyeni ife tichite zimenezo, pamene tikuweramitsa mitu yathu.

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,
Zizindikiro zimene Baibulo linaneneratu;
Masiku a Amitundu akutha, ndi zowawa
zitachulukana;

“Bwererani, O omwazikana, kwanu komwe.”

Tsiku la chiwombolo layandikira,
Mitima ya anthu ikulephera chifukwa cha
mantha;

Dzazidwani ndi Mzimu, nyali zanu muzikonze
ziziwala,

Yang’anani mmwamba, chiwombolo chanu
chayandikira!

Aneneri abodza akunama, Choonadi cha
Mulungu akuchikana,

Kuti Yesu Khristu ndi Mulungu wathu,
(Momwe izo ziriri zoonaa; oh, mazana!)

Koma tiziyenda pamene atumwi anayenda.

Pakuti tsiku la chiwombolo layandikira,
Mitima ya anthu ikulephera chifukwa cha
mantha;

Dzazidwani ndi Mzimu, konzani nyali zanu
ziziwala,

Yang’anani mmwamba, chiwombolo chanu
chayandikira!

²⁰⁵ Pamene inu muli ndi mitu yanu yoweramitsidwa, kodi ndi zoyenera kwa inu, mmawa uno, kuti inu mupereke moyo wanu kwa Khristu? Kodi Iye wayankhula kwa inu? Ngati ndi choncho, ingokwezerani dzanja lanu kwa Iye, ndi kuti, “Ine tsopano ndikumulandira Khristu. Izo ndizoyenera kwa ine kuti ndipereke zonse zanga, chifuniro changa, mmawa uno, kwa Iye. Ine tsopano ndikukweza dzanja langa ndi kuti, ‘Ambuye Yesu, ndichitireni chifundo.’ Ine ndikukusowani Inu, oh, momwe ine ndikukusowerani Inu! Ora lirilonse, ine ndikukusowani Inu.” Mulungu akudalitseni inu. “Oh, Mpulumutsi Wodala, ine ndikubwera kwa Inu.”

Ine ndikukusowani Inu, oh, ine ndikukusowani
Inu;

Bwanji ngati inu mukanakhala mutagona pamene amayi
agona tsopano?

Ora lirilonse ine ndikukusowani Inu!

Oh, ndidalitseni ine tsopano, Mpulumutsi
wanga,

Ine ndikubwera kwa Inu!

[M’bale Branham akung’ung’udza—Mkonzi].

(O Ambuye, ife tikukusowani Inu;)

Ora lirilonse ine ndikukusowani Inu!

Oh, ndidalitseni ine tsopano,

Ambuye, ndikukusowani Inu tsopano kuposa momwe
ndakhala ndikuchitira kwa nthawi yayitali.

Koma ine ndikubwera kwa Inu!

206 [M'bale Branham akuyamba kung'ung'udza, *Ine Ndikukusowani Inu Ora Lirilonse—Mkonzi*].

207 Atate Akumwamba, kutsika kupyola mu zigwa ife timayenda, tikudziwa kuti Inu munalonjeza, “Ine sindidzakusiyani inu, ngakhalenso kukutayani inu. Funani Ufumu wa Mulungu poyamba, ndi chirungamo Chake, zinthu zina zonse zidzawonjezedwa kwa inu.”

Kotero ine ndikubwera kwa Inu!

208 Ngati alipo ena pano, Ambuye, amene sali bwino mu solo zawo; ngati iwo akanakhala kuti amabwera mu njira imeneyo, imene amayi anga alimo pa miniti ino, O Ambuye, mulole iwo akhale ndi umboni umenewo, nawonso. Izo ndizokakamizika kwa ife lero, Ambuye.

209 Ife tiri pa mapeto a msewu, M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya; Uthenga; kukana kwa Uthenga; kutsimikizira kwa Uthenga; ndi Kukhalapo kwa Khristu akutsimikizira kuti Iye ali yemweyo, dzulo mmasiku a Loti, ndi mmasiku a thupi Lake, ndipo mmasiku a lero; dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

210 Aloleni iwo akulandireni Inu tsopano ngati Mpulumutsi wawo wodala. Perekani izi, Ambuye. Ine ndikupempha mu Dzina la Yesu.

Oh, ndidalitseni ine tsopano, Mpulumutsi
wanga,
Ine ndikubwera kwa Inu!

Ambuye wamtengo wapatali,
Mayesero amataya mphamvu zawo,
Zoonadi, Ambuye, pamene Inu muli pafupi.

Ine ndikukusowani Inu, oh, ine ndikukusowani
Inu!

211 Ngati Inu mwamutenga iye Ambuye, kapumitseni solo yake yamtengo wapatali Kumwamba. Perekani izi. Perekani izi, Ambuye.

Mpulumutsi wanga, Ine ndikubwera kwa Inu!

212 Atate Mulungu, timvereni ife. Ndichotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse pano. Ife tikudziwa chimene Mawu amanena. Ife sitiri mu mdima. Ife tikudziwa chimene Mawu analonjeza. Tithandizeni ife, O Ambuye, kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Akwaniritseni Mawu Anu. Mulole wokhulupirira aliyense pano akhale ndi chikhulupiriro tsopano, pamene ife tikubwera kwa odwala. Ife tonse timakonda kukhala moyo, Ambuye; koma choyambirira ndi kupeza Moyo Wamuyaya, wa dziko limenelo limene liri nkudza. Timvereni ife, Atate, pamene osonkhana akupemphera, makamaka odwala ndi osautsika aliyense.

213 Ine ndikudabwa, aliyense, ngati pali alendo aliwonse ndi ife, amene sanakhalepo mu kachisi, ndipo inu mukudwala, ndipo mukuyang'ana kwa Mulungu kuti akuthandizeni? Ndi mitu yanu yoweramitsidwa, nonse a inu. Kodi mungakweze dzanja lanu, anthu inu amene muli alendo kwa ine, amene simukundidziwa ine kapena ine sindikukudziwani inu, ndipo mwabwera kwa Khristu tsopano kuti mudzathandizidwe. Mungokweza mmwamba dzanja lanu. Mukuona? Mulungu akudalitseni inu, inu, ndi inu. Alipo angapo.

214 Inu muyenera kungokhulupirira. Uthenga uwu siuli pachabe, ndi Mawu a Mulungu.

215 Ndikuwona dona. . . Ndi mitu yanu yoweramitsidwa. Iye adakali chikwezere dzanja lake. Iye akusawutsika ndi vuto la mtima. Iye ndi Akazi a Nance. Iye akuchokera ku Madisonville, Kentucky. Uko nkulondola. Sichoncho, dona? Inu mukhoza kudzutsa mutu wanu ngati mukufuna. Inu munakweza dzanja lanu mmwamba, ndipo munangolisiya ilo mmwamba. Izo nzoona, sichoncho izo? Ngati izo ndi choncho, kwezani dzanja lanu. Mukuona pamene ife tikukhala, abwenzi? [Osonkhana akuti, "Inde."—Mkonzi]. Ine sindikumudziwa dona ameneyo. Ine sindinamuwonepo iye. Koma icho ndi chiyani? Ndi chizindikiro cha Uthenga. Kuti inu mukhoze. . .

216 Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, dona? Inu mukutero? Komabe, ndife alendo. Ine sindikukudziwani inu. Dzina limenelo linali lolondola, sichoncho ilo? Ngati ilo linali lolondola, chirichonse chimene Iye anakuuzani inu, mungo—mungobayibitsa manja anu kwa omvetsera, kuti iwo akhoze kuwona kuti izo zinali zoon. [Osonkhana akusangalala—Mkonzi].

217 Nchiyani chingachite zimenezo? Yesu waku Nazarete. Kuti inu mukhoze kudziwa kuti ndine mneneri wa Mulungu, ndipo ndikukuuzani inu Choonadi, pakuti chikutikakamiza ife. Mkazi anakhudza chovala Chake, ndipo Iye anatembenuka ndipo anamuuzza iye, lake "vuto la magari," ndipo anati linali litasiya.

218 Dona wakhala pafupi ndi inuyo, nayenso ali ndi vuto la mtima. Uko nkulondola. Eya. Ine sindikumudziwa iye. Inu mukudziwa kuti ine sindikudziwa, amayi. Koma Mulungu akumudziwa iye. Iye akudziwa vuto lake, sichoncho Iye? Akazi a Allen, kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchiritsani inu? [Mkaziyo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Ngati limenelo liri dzina lanu ndi vuto lanu, kwezani mmwamba dzanja lanu. Kwezani mmwamba dzanja lanu, ngati izo ziri zoon. [Osonkhana akusangalala.]

219 Dona wakhala pafupi ndi inuyo pamenepo. Ndikutanthauza Akazi a Bennett. Inu nonse ndi ochokera kumalo amodzi. Iye ali ndi vuto la impsyo mmalo mwa vuto la mtima. Inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza

kuchiritsidwa, nanunso. Kodi muchita zimenezo, dona? Kwezani mmwamba dzanja lanulo, ndipo munene kuti, “Ine ndikuvomereza zimenezo,” ndiye inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala bwino. Ngati inu mungakhoze kukhulupirira! Ndinu nonse aku Kentucky, mzinda wotchedwa Madisonville.

²²⁰ Akhala kumbuyo uko komwe, dona, Akazi a Bone. Iye amakhala pafupi ndi Madisonville. Iye samakhala mu Madisonville kwenikweni, iye akundiyang’ana kumene ine. Ndipo apo pali Mngelo uja wayima pafupi ndi iye. Iye amangokhala kufupi ndi Madisonville. Dzina lake ndi Bone; vuto la chimfine, vuto la mphumu, kukhosomola. Ngati uko nkulondola, bayibitsani dzanja lanulo mmbuyo ndi mtsogolo, dona. Mukhulupirire pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo mupite kwanu ndipo mukakhala bwino.

²²¹ Vuto laku mmero, bwana. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza vuto la mmero ndi kukupangani inu kukhala bwino? Muchiritsidwe! Mungokhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

²²² Abiti Hopkins, dona wachikudayo wochokera ku Chicago. Ine sindikukudziwa iwe, sindinakuwonapo iwe m’moyo wanga. Koma iwe ukufuna kuti uchiritsidwe ku manjenje amenewo, vuto la chimfine? Pita, ukhulupirire, ndipo ukhoza kukakhala bwino, nawenso.

²²³ Akazi a Hanes ochokera ku Columbus, Ohio. Inu mukhulupirire pa Ambuye Yesu Khristu, inu mukhoza kupita kwanu ndipo mukakhala bwino, nanunso.

²²⁴ Ife tiri panjira yakumapeto. Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, “Ameni!”—Mkonzi]. Ndizokakamizika kwa ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse. Iye analonjeza kuti zinthu zimenezo zikanadzakhalapo. Ife tiri pano. Kodi inu mukukhulupirira izo? [“Ameni!”]

²²⁵ Chabwino, ikani manja anu pa wina ndi mzake. Ine ndikufuna ndikufunsi inu funso. Kodi Yesu analonjeza kuti zinthu zimenezi zikanadzachitika m’masiku otsiriza? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. “Monga zinali m’masiku a Loti. Ntchito zimene Ine ndikuzichita, mudzazichita, inunso.” Kodi Iye ananenanso izi, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachiritsidwa?” [“Ameni.”] Kodi mwakonzeka kuti mutenge mayimidwe anu, wokhulupirira? [“Ameni.”] Pakuti ndichotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

²²⁶ Ndi chirungamo cha Mulungu, kuti pamene mipango iyi apa (imene ine ndikuyikapo manja anga, mu Dzina la Yesu) ikakukhudzeni inu; ine ndikudziwa Mzimu Woyera uli pano, Womwewo umene unali ndi Paulo. “Iwo ankatenga kuchokera kwa Paulo . . .” Koteru inu mudzachiritsidwa, ngati mudzangokhulupirira zimenezo.

227 Ine ndikukhulupirira Mzimu Woyera womwewo, Mzimu Woyera wa Baibulo, uli pano mmawa uno, ukudzitsimikizira Wokha, Uthenga wa mmasiku otsiriza, Mzimu Woyera waukulu Iyemwini, akudziwonetsera Yekha, kubwera mu thupi la munthu, kumachita ntchito Zake.

228 Ine ndayima mmawa uno, movutikira. Inu mukudziwa chimene ine basi ndikukonzekera kuchimva ndikachoka pano. Koma ndichotiyenera ife kuti chirungamo chonse chikwaniritsidwe.

229 Mulungu anayika Uthengawu pa mtima wanga. Tsopano ndizoyenera kwa inu, monga wokhulupirira, kuti mukhulupirire. Pamene inu mudakali ndi, manja anu pa wina ndi mzake, sipakhala munthu wodwala pakati pathu, ngati inu muti mungokhulupirira izo ndi mtima wanu wonse, konzekerani kutenga mayimidwe anu.

230 Tsopano, Atate Akumwamba, ife tikubweretsa kwa Inu omvetsera awa, utatha Uthenga uwu. Ambuye Mulungu, ndithudi anthu akhoza kuwona tsopano kuti izo ndi zoyenera kwa ife. Ndi zoyenera kwa mneneri, kuyima pa Mawu. Izo ndi zoyenera kwa membala wa mpingo, izo ndizoyenera kwa iwo kuti ayimirire. Izo ndi zoyenera kwa anthu odwala, kukhulupirira Mawu a Yesu Khristu, pamene Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachiritsidwa.”

231 Ine ndimati ndiyitane mzere wa pemphero umenewo, Ambuye. Koma uthenga umene wangobwera kumene kwa ine, pa lanya, wandigwedeza ine, Atate. O Mulungu, Mawu Anu amati, “Ndichotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.” Ndi awa apa, ayiyenera.

232 Mzimu Woyera uli pano kudzatsimikizira kuti Iye ali pakati pathu. Tsopano mulole Mphamvu ya Mulungu, mulole umboni wa Mzimu Woyera, usunthire mmitima ya anthu awa pakali pano, kuwapatsa iwo chitsimikizo; monga Daniele anali nacho, monga Nowa anali nacho, monga Enoki anali nacho, monga Yohane anali nacho, monga Petro anali nacho, monga Paulo anali nacho, monga Yesu anali nacho, monga Abrahamu anali nacho, monga onse a iwo anali nacho, Ambuye. Kuti, ndichotiyenera ife mu m’badwo uno, kumene mphamvu ya machiritso Auzimu ikutsanuliridwa, zizindikiro ndi zodabwitsa zikuchitika, kudzutsidwa kwakukulu kwabwera pakati pa anthu, Mzimu Woyera wagwera pakati pa anthu. Iwo afuula, ayankhula mmalirime, anenera, mphatso zazikulu, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Mngelo wa Uthenga, Mngelo wa m’badwo wawonekera kwa ife mmawonekedwe a Mzimu Woyera, ndipo Iye akutibweretsera ife Uthenga. Ife tikuwuwona Iwo ukukwaniritsidwa. Ife tikumuwona Iye akutenga matupi athu ndi kutisintha ife kuchokera kokhala anthu achivundi,

nkudzakhala nthumwi za Mulungu, kudzayankhula zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zachinsinsi. Pamene tikuwona zinthu izi, ndiye chikutiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

²³³ Pamene tikudziwa kuti Abrahamu anayang’ana mmbuyo kwa Loti, kuti pamene Daniele akanakhoza kuyang’ana kwa Abrahamu, kuti pamene Yohane akanakhoza kuyang’ana kwa Daniele, (O Mulungu!) kuti pamene Petro ndi Yohane akanakhoza kuyang’ana kwa Yesu. Ndipo pamene ife tingathe kuyang’ana kwa iwo, ndipo lero ife tikuwona zotsatira zomwezo pakati pathu, ndiye ndichotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

²³⁴ Mulole Mphamvu ya Yesu Khristu iyatse chipinda chino, ndi chikhulupiriro Chaumulungu, ndi kudzamuchiritisa munthu aliyense muno, ku kusautsika kulikonse ndi mthenda iliyonse, Ambuye. Ndipo, monga wantchito Wanu, ine ndikumulamulira mdierekezi uyu amene wakhala akukankhira pa ine mmawa wonse, amene wakhala akuyesetsa kuti andipangitse ine ndichoke pa guwa ili! Mwa chisomo cha Mulungu, ine ndinakhala pano, chifukwa cha zivundi zosauka izi, zodwala kapena—kapena zovutika za Mulungu.

²³⁵ Tuluka mwa iwo, Satana, mdierekezi iwe! Ndikukulumulira iwe, mwa Yesu Khristu Mulungu wamoyo, kuti uchoke kwa anthu awa, ndipo usadzawavutitsenso iwo, pakuti iwo akuyima monga ana a Chihebrei mu ora la kuyesedwa, kuti atenge mayimidwe awo, ndi kuchiritsidwa kuyambira ora ili mpaka mtsogolo. Kudzera mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikulumulira matenda ndi ziwanda mwa osonkhana awa, zimene zabwera kudzawadwalitsa anthu awa, kuti zichoke mwa iwo!

²³⁶ Ndi mitu yathu ili yoweramitsidwa, mitima yathu ili kwa Mulungu, ine ndiyimba nyimbo. Ine ndiyesera iyo, ndi thandizo lanu ndi thandizo la Mulungu. *Chikhulupiriro Changa Chikuyang’ana Kwa Inu*. Ine sindikufuna kuti inu mukayikire, ngakhale pang’ono, koma ine ndikufuna kuti inu mukhulupirire tsopano. Ndichotiyenera ife. Ndi Akhristu angati ali muno? Kwezani manja anu, ndipo munene, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni!”—Mkonzi]. Ndi okhulupirira angati? Nenani, “Ameni.” [“Ameni!”] Ndi angati mwayika manja anu pa ena? Nenani, “Ameni.” [“Ameni!”] Ndiye ndichotiyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.

Chikhulupiriro changa chikuyang’ana kwa
Inu,
Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi waumulungu;
Tsopano ndimveni pamene ndikupemphera,
Tengani zolakwa zanga zonse. . . (Tsopano,
tchimo ndi “kusakhulupirira”)
Oh ndiroleni ine kuyambira lero

Ndikhale Wanu kwathunthu!

Pamene mmoyo wamdima ndiyenda,
Ndipo nkhwawa zindizinga mozungulira,
(Mulungu, khalani Namulondola wanga
tsopano!)

Khalani Inu Namulondola wanga;
Lamulani mdima ukhale usana,
Pukutani misozi yachisoni,
Ndiponso musandirole ine kuti ndidzachoke
ku mbali Yanu.

²³⁷ Ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Amayi anga okonedwa achikulire amenewo amwalira kuyambira pamene ndakhala ndikulalikira, mulole liwu langa likamvekere uko kudutsa mu zigwa zazikulu za Kumwamba.

²³⁸ Pamene iwo anandiuza ine, tsiku lina, iwo anati, “Billy, iwe wakhala ukundidyetsa ine. Iwe wakhala ukundilipirira lendi ndi ngongole yanga yo pepuka, kundipatsa chinachake choti ndidye.” Anati, “Wokonedwa, pamene iwe unali mnyamata wamng’ono, ine ndinkatuluka kunja mu nyengo ndi kukadula nkhuhi, ndinkakuyatsira iwe moto kuti uzitenthedwa. Ndipo ndinkakuphikira iwe, zomwe tinali nazo mnyumbamo, kuti tiphike.” Kuwawona iwo atagona pamenepo, ndi manja aang’ono ofooka amenewo amene ankachapa zovala zathu zakuda. Inu mwayima opanda thandizo, palibe chimene ine ndikanakhoza kuchita.

²³⁹ Ine ndinati, “Amayi, m’manja mwa Mulungu wamoyo, ine ndikupereka moyo wanu wolungama.”

²⁴⁰ Ngati iwo apita kuyambira pamenepo; onse a iwo anapita, azichimwene anga ndi onse amene atsalira. Uthengawu apa pa guwa unali woyipa kwambiri. Ngati iwo apita, Mulungu apumitse solo yawo. Ngati iwo akadali ndi ife, ndikukhala ndi ife mpaka usikuuno, mwa chisomo cha Mulungu ine ndikhala pano pa guwa kuti ndikwaniritse ntchito yanga, pakuti ndichondiyenera ine kuti ndikwaniritse chirungamo chonse.

²⁴¹ Pamene ine ndikufufuza, ine ndikupereka msonkhanowu kwa M’bale Neville, m’busa wanga wothandizira wodalitsika.



61-1001M Ndichotiyenera Ife Kuti
Tikwaniritse Chirungamo Chonse
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org